BUKHU

{LOMASULIRIDWA}

LA

CHIVUMBULUTSO

BUKHU 1
[CHAPUTALA 1-3]

Kwa
Mkwatibwi wa Khristu
Bukhu ili laperekedwa

BUKHU {LOMASULIRIDWA} LA CHIVUMBULUTSO

Ben Howard

Translated To Chichewa Language
By
Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza-Malawi

KUSINDIKIZIDWA KOYAMBA 1980

KUSINDIKIZIDWA KACHIWIRI 2005

Palibe gawo la bukhu ili limene lingachulukitsidwe [kupatula lemba la Baibulo] popanda chilolezo cholembedwa. Kuti mumve zambiri lemberani ku:

Sound of Liberty
Ben Howard
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534

TwoAnds@soundofliberty.org
www.SoundofLiberty.org

MALONJE

Bukhu la Chivumbulutso ndi bukhu la zoimirira, limene; politanthauzira, ndi uneneri wapamwamba. Ili si bukhu limene likuchita ndi chiphunzitso kapena ziphunzitso za maziko zimene zinabwera kwa ife ndi mtumwi Paulo ndi alembi ena a malemba za m'mene tingapulumutsidwire kapena m'mene tingalandirire dongosolo la chipulumutso la Mulungu.

Bukhu la Chivumbulutso linalembedwa mu 96 A.D. mpingo utagwa ku chikondi chake choyamba. [Chivumbulutso 2:4] Chikuonetsa m'mene mpingo unathera kudutsa mu nthawi mu maonekedwe ake akugwa. Chikuonetsanso [ndipo mofunika kwambiri] mpingo ukubwezeretsedwa ku malo ake a pachiyambi kuno ku nthawi yotsiriza.

Mpingo wapachiyambi sunagwe kuchokera ku bukhu la Chivumbulutso, chifukwa sunali gawo la malangizo wolembedwa kwa mpingo kuchiyambi. Ndi bukhu la mwala wapangodya, ndipo osati bukhu la maziko, ndipo kotero ndilongomasuliridwa kwa mpingo pano pa nthawi yotsiriza. Ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa mkwatibwi, ndipo Khristu akupanga chikondi ndi mkwatibwi wake pamene Iye akumupatsa iye mzimu wa vumbulutso ndi kuulura zinsinsi kwa iye. Ichi ndi chifukwa cha bukhuli, **"Bukhu [lomasuliridwa] la Chivumbulutso."** Ndi Mulungu kuika Chisomo Chachikulu [Machitidwe 4:33] pa mpingo wake mkwatulo usanachitike.

Komanso, mundirole ndilankhule, kuti owerenga ambiri a bukhu la Chivumbulutso alakwitsa potenga Yohane, mlembi, ngati Yohane nkonzi wa bukhu. Koma palibe njira iliyonse tinganene molondora kuti Yohane ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso. Iye anali mlembi, chotengera chabe chimene Mulungu anagwiritsa ntchito kufalitsa malingaliro Ake ku Mau olembedwa kuti awuluridwe pano mu nthawi yotsiriza. Yesu anali, ndipo ndi nkonzi wa bukhu la Chivumbulutso.

Momwemonso olemba bukhu ili akuzindikira mochuluka kuti NKONZI wa bukhu la Chivumbulutso ndi amene wapereka kudzoza kwa kumasulira kwenikweni kwa mlembi uyu. Kotero, ine ndikupemphera kuti mwapemphero inu mutenga kumasulira kwa bukhu la Chivumbulutso chifukwa mkwatibwi wa Khristu adzamvetsa bwinobwino zimene zikuchitika pano mu nthawi yotsiriza, chifukwa kuwala kwake [kumvetsa] ndi kowala ngati krustalo. [Chivumbulutso 21:11]

Komanso, ndiloreni ndinene ine -Ben Howard- kuti: kwa zaka zoposa 45 ndakhala ndikutumikira pa zolembedwa zimene zili mu bukhu ili, ngati mishonare mu maiko ambiri ndi kuno ku USA, mu mipingo, maholo, madera, nyumba zobwereketsa, ngati mlaliki wa pa wailesi, kufunsidwa mafunso, ndipo tsopano pa Internet, ngati m'busa wa **Sound of Liberty Assembly** moyandikana ndi Dawsonville, Georgia [USA] ndi mitundu ina ya malo wopezekamo anthu. Mwambiri mwa malo olankhulawa, kufunsidwa mafunso ndi zina, panali kujambulidwa matepi komanso kutenga mfundo zolemba pa zimene zimalankhulidwa zimene ine tsopano sindingathenso kuzilamulira.

- Kotero, zidziwike kwa onse: Kuti bukhu ili lapambana, ndipo laposa, zolembedwa zonse, zojambulidwa kapena mitundu ya nkhani zonse zotengedwa kuchokera kwa mlembi zimene zikuoneka ngati- kapena- zikutsutsana ndi zolembedwa izi, ngati zimenezo zinatengedwa mbuyomu lisanasindikizidwe bukhuli.
- Ichi ine ndikunena, chifukwa maulaliki ambiri pa matepi, ma CD, ma DVD, ma Video, komanso pa Internet apita ku madera ambiri padziko lonse kwa zaka zambiri zimene muli zochepa, ndipo mauthenga ena akale akhoza ngakhale kutsutsa zolemba izi, ine ndachita monga 2 Petro 3:18 amatiphunzitsa ife kuti *"Kukula mu chisomo ndi chizindikiritso cha Ambuye wathu."*
- Kotero, ine ndinena kwa inu kuti ine ndakhala mu utumiki uwu kwa zaka zambiri, monganso inu amene mukuwerenga ichi kwa nthawi yoyamba, kuti bukhu ili lidzapereka kuwala kwakukulu ku "Bukhu la Chivumbulutso" kusiyana ndi mauthenga anga akale amene inu mukhoza kukhala nawo, kaya pa tepi, kulembedwa mwa bukhu, kapena zolemba zanuzanu pa zimene mlembi anapereka, kaya zaka 45 zapitazo kaya zaka 5 zapitazo.

- Ichi ndikunena, chifukwa mzimu womwewo wa Chivumbulutso umene unamupangitsa Yohane kulemba Bukhu la Chivumbulutso wapangitsa kuti limasuliridwe pano mu nthawi yotsiriza kwa Mkwatibwi Wake.

Izi ndikulankhula mokhudzana ndi bukhu lonse la Chivumbulutso, ndipo silinapangidwe pa cholinga chochotsapo vumbulutso lililonse limene Mulungu akanapereka patsogolo kwa ine kapena wina aliyense wa atumiki woona wa Mulungu pa Bukhu la Chivumbulutso. Inu mukhoza kukhala otsimikizika kuti vumbulutso lenileni silidzatsutsana ndi zolemba izi.

Posachedwa, utumiki onse woona udzaoneka diso kwa diso [1 Akorinto 1:10] pa kumasulira uku pamene liwu la vumbulutso la Mulungu liyamba kulankhula kuchokera kumwamba mu kufotokoza kwakukulu mwa Mzimu Wake [Chivumbulutso 10:8] pa zinthu zimene mukufuna muwerenge.

Ndikupempheni inu owerenga, kuti muzindikire kuti zolembedwa izi ndi za okhawo amene ali ndi makutu auzimu kuti amve chimene Khristu akunena kwa mkwatibwi wake pamene Iye akupanga chikondi ndi iye, chifukwa Bukhu la Chivumbulutso ndi kalata wa chikondi wa Mulungu kwa Mkwatibwi.

Kotero, mukatha kuwerenga bukhu ili, ngati silingadzutse wamkati wanu ndi kuwalira moyo wanu, ndiye pepani potenga nthawi yanu, ndipo chonde perekani bukhu ili kwa wina aliyense chifukwa chowaganizira mwa pemphero, mwina ndi lawo. Ine ndikukuthokozani mokoma chifukwa cha nthawi yanu ndi mgwirizano.

Pemphero langa kwa inu owerenga ndi ili: *Mulungu akupatseni inu mzimu wa nzeru ndi chidziwitso, ndi kuti maso akumvetsa kwanu awunikiridwe. Kuti mukamvetse masamba otsatira a bukhu ili. Bukhu ili likuthandizeni kuti muvale chovala choyera [Chivumbulutso 19:7-9], kuti musandulike mkazi wa Khristu pokhala m'modzi ndi Mau Ake munthawi yotsiriza iyi. Amen.*

Kuthokoza Kwapadera Kwa …

Ine ndikufunanso ndiwonetsere kuyamikira kwanga pa
ntchito
ya malemu William M.Branham mneneri wa Mulungu
wam'thenga
wa m'badwo uno wa Laodikaya komanso malemu mtumwi
Raymond M. Jackson
amene Mulungu anamugwiritsa ntchito kuti apitirize ntchito Yake imene Iye anaiyamba kupyolera mwa William Branham; makamaka mu gawo la mbiri la bukhu ili. Ngakhale ife sitili othandizidwa, kapena kukwezedwa ndi otsatira a
aliyense
wa uthenga wa amuna amenewa; zolemba zawo zinali zothandiza kwambiri pokonza bukhu ili.

Komanso, kuthokoza kwa padera kwa

Joyce Howard
Gary Gentry
Wanda Robertson
Barbara Howard
Leah Farruggia
ndi Enoch Kamanula

chifukwa cha kuthandiza mosatopa pa ntchito iyi.

"Ndipo anadza m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri akukhala nazo mbale zisanu ndi ziwiri, Nalankhula ndi ine, nanena, Idza kuno, ndidzakuonetsera iwe…" Chivumbulutso 17:1.

Lemba la pamwambali likuonetsa m'modzi mwa angelo asanu ndi awiri amene akulankhulidwa kudutsa mu bukhu lonse la Chivumbulutso. M'modzi wa iwo akumuonetsa Yohane, amene akuimirira utumiki ngakhalenso kuimirira mkwatibwi, bukhu la Chivumbulutso. Kuona angelo asanu ndi awiri ndi kumvetsa ntchito zawo zimene iwo amachita ndi zinthu zopindula ku kumvetsa kwanu ku bukhu la Chivumbulutso. Izi zatsimikizidwa mu bukhu lonseli ngati chifungulo chenicheni chotsekula zinsinsi za [zoyamba] bukhu lozwizwitsa la Chivumbulutso.

MALONJE KU CHAPUTALA CHILICHONSE

Chaputala Choyamba

Chaputala choyamba cha bukhu la Chivumbulutso chikutionetsera poyera chithunzithunzi cha Umulungu. Chinayamba ndi mau awa: *"Chivumbulutso cha Yesu Khristu, chimene Mulungu anampatsa Iye."* Choncho, mu chaputala choyamba tikuchita koyambirira ndi Mulungu [Mzimu wa muyaya] ndi Yesu Khristu mwana wa Mulungu. Inu mudzakhoza kumvetsa Umulungu pamene muwerenga chaputala ichi. Chaputala ichi chikuonetsanso mpando wa chifumu, mizimu isanu ndi iwiri, Yohane pa chisumbu cha Patmo, mipingo isanu ndi iwiri yaku Asia, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri, amene ndi amithenga asanu ndi awiri a pansipano ku mipingo isanu ndi iwiri yaku Asia, imene imaimirira mibado isanu ndi iwiri ya mpingo ndi amithenga asanu ndi awiri.

Angelo auzimu asanu ndi awiri kapena mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu, pa mpando wachifumu, akuoneka kwa nthawi yoyamba mu Chipangano Chatsopano mu chaputala choyamba vesi 4. Angelo asanu ndi awiri ali ndi gawo lofunika mu dongosolo la chiombolo mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Iwo ali ndi ntchito zosiyanasiyana zoti achite. Choyamba, iwo ndi angelo auzimu ku mibado ya mpingo, iwo ali ndi zisindikizo, iwo ndi mabingu, iwo amaimba malipenga ndikutsanula miriri, mwa zina. Izi zafotokozedwa mumachaputala ena, kotero mu chaputala choyamba, Umulungu ndi phunziro lofunika kwambiri. Si **"Yesu yekha,"** kapena **"Utatu"** monga m'mene chaputala choyamba chikuonetsera.

Chaputala Chachiwiri

Chaputala chachiwiri chikutionetsera ife chithunzi cha mpingo, osati monga m'mene zinaliri pa Pentekosite mu 33 A.D; koma monga zinalili kuchokera mu 66 A.D. mpaka 1520 A.D. ndipo zikudutsa mibado ya mpingo inayi yoyamba.

Bukhu la Machitidwe likuonetsa mpingo kuchokera mu 33 A.D. mpaka 66 A.D. Iyi inali nyengo ya nthawi imene Khristu anatsogolera mpingo wake; usanagwe kuchokera ku mau enieni ndiponso tirigu ndi nansongole zisanaloredwe kukulira limodzi, ndipo Khristu amayenera kuchotsa chidzalo chake cha Iye yekha ku mpingo ndi kutsogolera mpingo wake pogwiritsa ntchito angelo auzimu asanu ndi awiri kuti apereke Mau Ake ku mpingo wake wa ku mibado isanu ndi iwiri ya mpingo, mpakana Iye atabweranso mu Chivumbulutso Chaputala 10. Komanso, panali munthu m'modzi mu m'bado uliwonse amene anaima kuchokera kwa azitumiki ena amene mngelo wauzimu amamugwiritsa ntchito kuti alalikire mau a mu m'bado umenewo kwa anthu, ndiye iye anakhala **nyenyezi** ya m'bado umenewo, monga mwaphunzirira mu bukhu ili. Ndiloreni ndinene apa, kuti mipingo isanu ndi iwiri inalipo ndithu mu tsiku la Yohane ndipo panali amuna asanu ndi awiri [Abusa] amene, mizimu isanu ndi iwiri [angelo] amatumikirapo, ndipo izi zinaika kachitidwe ku mipingo isanu ndi iwiri.

Chaputala Chachitatu

Chaputala chachitatu chikutionetsera ife mibado itatu ya mipingo yotsiriza, kubadwa, moyo ndi kufa kwa chiprotestant, chimene monga mwa malemba ndi ana akazi a hule mai wamkulu. [Chivumbulutso 17:5] Iyi ndi nthawi ya kukonzanso pamene Mulungu amayamba kubwezeretsa choonadi ku mpingo wake woona, koma mu m'bado uliwonse iwo amapanga bungwe ndi kupanga chipembedzo. Wotsutsa

khristu amatenga ulamuliro wa mipingo ya bodza, pamene mpingo woona wa Mulungu unayenda ndi Mau monga mukhoza kuona mu chaputala ichi chikudutsa nyengo ya nthawi kuchokera 1520 A.D. mpakana ku mapeto, monga Mulungu akupha ana [mipingo ya chiprotestant] ndi hule wamkulu ndi imfa yauzimu, ndikuwaponya iwo mu nyengo ya chisautso.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHOYAMBA

Vesi 1: *"Chivumbulutso cha Yesu Khristu, chimene Mulungu anamuvumbulutsira achionetsere akapolo ake, ndicho cha zinthu izi ziyenera kuchitika posachedwapa; ndipo potuma mwa mngelo wake anazizindikiritsa izi kwa kapolo wake Yohane."*

Vesi 2: *"Amene anachita umboni za mawu a Mulungu ndi za umboni wa Yesu Khristu, zonse zimene adaziona."*

Ife tiphunzira mu chaputala choyamba cha Chivumbulutso za Mulungu ndi Yesu. Inu mukhoza kufunsa, "Kusiyana kwake ndi kotani?" Tikhoza kunena kuti ichi ndi chinthu chimodzi. Palibe amene adamuona Mulungu. Iye ndi wosaoneka, Mulungu ndi Mzimu; koma Yesu Khristu wakhala ali pano ngati munthu ndipo amatha kuoneka, koma Mulungu anakhalabe Mzimu ngakhale pamene Yesu anali pano ngati munthu.

Chifukwa chiyani Mulungu anamupatsa Yesu Khristu vumbulutso? Apa pali chifukwa chake: kuti akaonetsere akapolo ake zinthu zimene ziyenera kuchitika posachedwapa, Iye akufuna kuwala kwa uthenga kuwale. Ichi ndi chifukwa chimene Mulungu anapatsa Yesu vumbulutso, ndipo Yesu anapereka kwa Yohane, ndipo laperekedwa kwa ife kupyolera mu zolemba za Yohane. Ndipo tsopano, pano mu nthawi yotsiriza, Mulungu watitumizira ife kutanthauzira kwake.

Kumasulidwa kwa bukhu la Chivumbulutso ndi kwa mkwatibwi wa Yesu kuti amvetse. Ngakhale sitikhala pano pamene gawo lalikulu la bukhu la Chivumbulutso likuchitika, Mulungu akufuna ife kuti tidziwe zimene zili mu bukhu la Chivumbulutso, ndipo zili mu bukhu ili.

Vesi 3: *"Wodala iye amene awerenga, ndi iwo amene amva Mau a chinenero nasunga zolembedwa momwemo, pakuti nthawi yayandikira."*

Mulungu amadziwa kuti zidzatengera kuwerenga mbiri kuti mumvetse bukhu la Chivumbulutso. Kotero, poti zimatengera kuwerenga mbiri pamodzi ndi Baibulo kuti mumvetse bukhu la Chivumbulutso, kotero zoonjezeredwa mu bukhuli ndi mbiri kuti itithandize ife kumvetsa zimene Mulungu akutionetsera.

Vesi 4: *"Yohane kwa mipingo isanu ndi iwiri mu Asia: Chisomo kwa inu ndi mtendere, zochokera kwa Iye amene ali ndi amene adali ndi amene alinkudza; ndi kwa mizimu isanu ndi iwiri yokhala ku mpando wachifumu wache."*

Apa tikuyamba kuona chinsinsi chimene sichinatchulidwepo mu Chipangano Chatsopano. Iyi ndi nthawi yoyamba mizimu isanu ndi iwiri ikutchulidwa mu Chipangano Chatsopano. Ndizofunika kudziwa kuti ichi sichinalembedwepo, mpakana mu 96A.D, zaka makumi atatu Paulo atamwalira. Izi zikhala zofunika patsogolo mu bukhuli.

Tsopano tayang'anani mu vesi ili, *"mizimu isanu ndi iwiri yokhala pa mpando wa chifumu wa Mulungu."* Izi zikumveka zodabwitsa sichoncho? Chifukwa paliponse pamene Paulo amalankhula za Mzimu wa Mulungu, iye anati, "Mzimu umodzi, Ambuye m'modzi, Chikhulupiliro chimodzi, Ubatizo umodzi, ndi Mulungu m'modzi." Koma pano, Yohane, **zaka makumi atatu Paulo atapita**, anayamba kulemba za mizimu isanu ndi iwiri.

Mizimu isanu ndi iwiri imaimirira angelo auzimu asanu ndi awiri pa mpando wa chifumu, kuti atenge ntchito ndi utumiki wa Yesu Khristu mpingo utagwa ku chiyero. Izi zinachitika Yohane asanalembe mu 96A.D.

Angelo asanu ndi awiri awa ali ndi ntchito zosiyanasiyana zoti achite, zimene zikuphatikiza mibado ya mipingo, zisindikizo [ndikumasulira kwake, kumene ndi kumveka kwa mabingu apa Chivumbulutso

chaputala 10], mabingu asanu ndi awiri, ndi miriri isanu ndi iwiri yotsiriza monga anaonetsera Yohane ndi kuziulura mu bukhu ili. Monga mwaonera mu chaputala ichi, Khristu akuoneka ngati wamsembe wankulu, ndipo osati Mzimu Woyera ngati m'mene zinalili pa chiyambi cha mpingo. Ku Machitidwe, chaputala 2, Iye akubwera ngati Mzimu Woyera kwa Ayuda, ndipo akubweranso mu njira yomweyo kwa Amitundu ku Machitidwe, chaputala 10. Ndizofunika kudziwa kuti mpingo unagwa ku chikondi chake choyamba…, onse Ayuda koyamba kenako Amitundu. Zitatha kuchitika izi, Khristu sakuoneka ngati Mzimu Woyera mwa njira yapamwamba koma udindo wapamwamba ndi wa Wamsembe Wankulu.

Khristu atakhala Wansembe Wankulu, angelo awa anatumikira mu zotengera za pansi zimene zinaikidwa kulalikira uthenga wa nthawi yawo. Nyengo ya nthawi imeneyi ikutchedwa "Ufumu wa kumwamba," ndipo ikuimirira nthawi yolembedwa ku Mateyu Chaputala 13, pamene tirigu ndi namsongole zaloledwa kukulira limodzi, pamene Khristu ndi Wansembe Wankulu kuimirira ana ake.

Mafanizo asanu ndi awiri aku Mateyu, chaputala 13, akuimirira mibado isanu ndi iwiri ya mipingo, imene angelo asanu ndi awiri auzimu akutumikira kwa amithenga apansi pano pamene Mulungu akuchita ndi mibado isanu ndi iwiri ya mipingo kuti aipatse kuwala. Chaputala 2 ndi 3 cha Chivumbulutso chikudutsa mu nyengo yomweyi.

Musaphonye izi: **Khristu samaoneka ku mpingo woyamba ngati kuti akugwiritsa ntchito mizimu isanu ndi iwiri.** M'malo mwake, mpingo makamaka gawo la Amitundu, linali thupi la Khristu pa dziko, ndipo Khristu anali atayamba kulankhula kupyolera mu utumiki wake wa ku Aefeso 4:11, mpingo wake usanagwe ku Mau Ake ndipo unachotsedwa ku madalitso athunthu a Mulungu.

Tsopano, uyu ndi ndani *"amene anali ndi amene alinkudza?"* Yohane analandira moni wochokera kwa Iye: *"Chisomo chikhale pa inu, ndi mtendere, zochokera kwa Iye amene ali ndi amene alinkudza."* Izi zikuimirira Mulungu wamuyaya osati Yesu Khristu; chifukwa Mulungu alibe chiyambi, komaYesu anali. Mulungu anali nthawi zonse, Iye ali ndipo adzakhala nthawi zonse, **komaYesu anali ndi chiyambi ngati munthu.**

Vesi 5: "*Ndi kwa Yesu Khristu, mboni yokhulupilikayo, wobadwa woyamba wa akufa, ndi nkulu wa mafumu a dziko lapansi. Kwa Iye amene anatikonda ife, natimasula ku machimo athu ndi mwazi wache."*

Pachifukwa chakuti Yesu ndi wobadwa woyamba wa akufa zikutanthauza kuti padzakhala enanso amene ali wobadwa a akufa. Taonani ichi: Pamene tiuka mu chiukitsiro, kapena pamene tisandulika, ife tidzakhala chimodzimodzi monga Iye ali tsopano. Iye ndi mwana wa Mulungu tsopano ndi thupi la ulemelero, ndipo ife tikhala ana amuna a Mulungu ndi matupi a ulemelero.

Moni ameneyu wachokera kwa *"Iye amene ali, ndi amene anali ndi amene alinkudza; ndi kwa mizimu isanu ndi iwiri yokhala ku mpando wa chifumu wake, ndi kwa Yesu Khristu."*

Vesi 4 ikuonetsa Mulungu wa muyaya ndi angelo asanu ndi awiri auzimu, koma vesi 5 ikuonetsa mamuna Yesu Khristu. Pamene mau akufutukuka ife tikuona mamuna Khristu Yesu ndi Mulungu ali amodzi, **pamene zimvetsedwa molondora.** Paulo anati Mulungu anali mwa Khristu kuyanjanitsa dziko kwa Iye mwini. [2 Akorinto 5:19]

Mu ulamuliro wa Mileniamu Yesu Khristu adzalamulira ngati Mfumu. Ulamuliro wa Mileniamu ukatha Iye adzakhala pa mpando wachifumu ndipo adzakhala Oweruza. [Chivumbulutso 20:11-15] Kenako adzapereka ufumu kwa Mulungu amene anamupatsa Iye, [1 Akorinto 15:24-28], ndipo Mulungu adzakhalabe, " Iye amene anali, amene ali ndi amene alinkudza," koma Yesu Khristu adzakhala nafe mu maonekedwe a thupi, pamene Iye ndi Mulungu Atate akhala amodzi, kupanga Khristu gawo lowoneka la Mulungu. [Chivumbulutso 22:3, 4]

Kumbukirani, thupi la Khristu la **Yesu Khristu linali ndi chiyambi.** Linayamba tsiku lija ku Nazareti pamene mngelo anaonekera kwa namwali Maria ndikunena kuti iye anakonderedwa mochuluka ndi Mulungu ndipo adzakhala ndi pakati, ndikubereka mwana, ndikumutcha dzina lake Yesu. Maria anati, "Izi zidzachitika bwanji powona kuti sindidziwa mamuna? "Ndipo mngelo anati zidzachitika mwa Mzimu wa Mulungu**. Icho chinali chiyambi cha Yesu Khristu ngati munthu.** Koma Mulungu anali nthawi zonse, Iye ali tsopano, ndipo Iye adzakhala nthawi zonse. Pamene Yesu Khristu sakhalanso pa mpando

wa chifumu mu ulamuliro wa Mileniamu ngati mfumu, Mulungu adzakhalabe Mulungu. Iye adzakhalabe wa muyaya. Pamene Yesu Khristu sakhalanso ngati Oweruza kuweruza mtundu wa anthu, Mulungu adzakhalabe wa muyaya. **Iye ndi Mzimu ndipo Iye nthawi zonse adzakhalabe Mzimu.** Munthu wa pansi uyu, Khristu Yesu, anali ndi chiyambi monga mukuonera tsopano, koma Mulungu, Mzimu wamuyaya, unalibe chiyambi.

Tsopano gawo lotsiriza la vesi 5 likuti Yesu Khristu anatitsuka ife ku machimo athu ndi mwazi wake. Iye analalikira pafupifupi zaka zitatu ndi theka ndi kufa pa mtanda, kutitsuka ife ku chikhalidwe chathu cha uchimo, ndikutipanga ife oyera ndi mwazi wake wapamwamba. Tsopano, kuti chikhalidwe chathu cha uchimo chayeretsedwa mwa imfa ya Khristu pa mtanda, chinthu chotsatira mu dongosolo la chiombolo chathu ndi kumvera ulamuliro wa Yesu waku Mateyu 28:19, mu dongosolo limene Petro ndi atumwi ena anamvera pa tsiku la Pentekosite. Njira yabwino kuti izi zichitike ndi mwa chitsanzo cha atumwi, Machitidwe 2:38; chifukwa iwo anamvetsa kuti Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera anali maudindo ndipo osati dzina. Choncho Petro atatsegula chitseko cha ku ufumu wa Mulungu, iyi inali njira yokhayo imene ubatizo wa m'madzi unayang'aniridwa *"Koma Petro anati kwa iwo, lapani batizidwani yense wa inu mu dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha **machimo** anu; ndipo mudzalandira mphatso ya mzimu woyera,"* POKHAPO potsata njira iyi inu mukhoza kunena mwauzimu inu mwatsukidwa ku machimo anu ndipo mukubadwa mwatsopano mwa Baibulo. Akatha masitepe amenewa tikupitirira ku ungwiro, kapena kukula msinkhu, mwa kuyenda mu kuwala kwa Mau Ake; ndipo mwazi wake umapitirira kutiyeretsa ife ku zolakwitsa zathu. [1 Yohane 1:4-10]

Vesi 6: *"Natiyesa ife mafumu ndi amsembe a Mulungu ndiye Atate wache, kwa Iye kukhale ulemelero ndi mphamvu kufikira nthawi za nthawi. Amen."* Uku ndi ku Mileniamu.

Yemweyo amene ali Atate a Yesu Khristu ndi Atate wathu.Yohane 20:17- *"Ndikwera kunka kwa Atate wanga,ndi Atate wanu, ndi Mulungu wanga, ndi Mulungu wanu."*

Pamene Yesu anagonjetsa ndi kulandira malo ake ndi Atate, ifenso tidzatero ngati ogonjetsa kulandira malo athu ndi Khristu mu ufumu wake chifukwa chokhala ogonjetsa pano mu moyo uno.

Vesi 7: *Taonani, adza ndi mitambo; ndipo diso liri lonse lidzampenya Iye, iwonso amene anampyoza; ndipo mafuko onse a padziko adzamulira Iye. Terotu, Amen.*

Vesi ili likukamba za munthu wathupi, Khristu Yesu, kubweranso, chifukwa palibe munthu amene angaone Mulungu, chifukwa Iye ndi Mzimu. **Njira yokhayo imene inu mungaonere Mulungu ndi kuona ntchito za Mulungu,** koma diso lililonse lidzamuona munthu ameneyi Yesu Khristu, akubweranso. Vesi ili silikukhudzana ndi mkwatulo wa mpingo woona, chimene chidzakhala chinsinsi monga m'mene dziko likudziwira za izo. *"Diso lililonse lidzampenya Iye,"* tiyeni tidziwe kuti uku ndi kubwera kwa Khristu mu thupi chitatha chisautso chachikulu. Mateyu 24:29-30 ndi Chivumbulutso 6:14]

Vesi 8: *Ine ndine Alefa ndi Omega, oyamba ndi otsiriza ati Ambuye Mulungu,amene ali, amene adali, ndi amene alinkudza, Wamphamvu zonse."*

Ine ndikufuna inu muone apa m'mene Mulungu ndi Yesu alili amodzi, ndi kumvetsa kolondora. Apa, Yesu Khristu akuchibweretsa kuti Iye ndi Mulungu. Mwa Yesu Khristu mumakhala chidzalo chonse cha thupi la Umulungu. Zonse zimene tikuti tione za Mulungu muthupi, zonse zomwe tikuti tidziwe za Mulungu mu moyo wake, zakutiridwa mwathupi mwa Yesu Khristu; koma Mulungu adakali Mzimu wa Muyaya wopezeka paliponse nthawi yomweyo.

Vesi 9: *"Ine Yohane, m'bale wanu ndi woyanjana nanu m'chisautso ndi ufumu ndi chipiriro zokhala mwa Yesu, ndinakhala pa chisumbu chotchedwa Patmo, chifukwa cha Mau a Mulungu ndi umboni wa Yesu."*

Patmo ndi kachilumba kakang'ono kumene Aroma amaika olakwa, ndipo panalibe njira iliyonse yothawira. Inali yodzaza ndi ng'ona komanso njoka. Yohane anali atadutsa mu nthawi yovuta yokhala yekha. Iye anali munthu wokalamba pamene iye amaikidwa pa chilumba ichi, ndipo mosakaika mdierekezi anabwera kwa iye ndikumuuza iye kuti anali munthu wokalamba woiwalidwa ndipo akanafera pamenepo, koma Mulungu anali ndi chikonzero china! Mdierekezi anali atapanga kulakwitsa tsiku

limenero pamene anamuika Yohane pa chisumbu cha Patmo, chifukwa Yohane analibe chochita chilichonse koma kuyamika Mulungu ndi kulowa mu uzimu.

Nthawi zina Mulungu adzakhala ndi zochitika zina kufika poti sitingachite china chili chonse koma kuyamika Mulungu, kumukonda Iye, kutumikira Iye, ndikukhulupirira Mau Ake; monga m'mene Yohane anachitira pa chisumbu cha Patmo.

Taonani zimene zinamutengera Yohane kuti atenge Mau a Mulungu kwa ife. Chisautso ndi chipiriro zinali mphotho imene analipira chifukwa cha umboni wake wa Yesu Khristu. Ife tikupereka chiyani chifukwa cha ku masulira? Panali maora a ndekha ndekha operekedwa kukonza bukhu ili.

Vesi 10: *"Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye, ndipo ndinamva kumbuyo kwanga mau akulu, ngati a lipenga."*

Yohane anali mu Mzimu mpakana Mulungu anamutenga iye ndikumuika mu tsiku la Mileniamu ndi kumulora iye awone zonse izi mu bukhu la chivumbulutso zikukwaniritsidwa.

Baibulo likuti palibe chilichonse chatsopano pansi pa thambo.[Mlaliki 1:9] Mileniamu siyachilendo kwa Yohane, chifukwa iye anali kumeneko kale. Iye waona kale mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Palibe chachilendo ndi mabingu asanu ndi awiri, chifukwa Yohane waamva kale, chimodzimodzi ifenso, pamene zisindikizo zinatsegulidwa mu 1963. Ichi ndi chimene Chivumbulutso 10 chili.

Vesi 11: *"Ndikuti, Ine ndine Alefa ndi Omega, oyamba ndi otsiriza: ndipo, chimene upenya, lemba m'bukhu,nulitumize kwa mipingo isanu ndi iwiri, ku Efeso, ndi ku Smurna, ndi ku Pergamo, ndi ku Tiyatira, ndi ku Sarde ndi ku Filadelfeya ndi ku Laodikaya."*

Gawo loyamba la vesi ili likuonetsa Umulungu wa Yesu Khristu umene Mulungu waika mwa Iye. Kotsatira kwa vesi ili akumuuza Yohane kuti alembe zimene anaziona mu bukhu ndikuzitumiza ku mipingo isanu ndi iwiri ku Asia. Mipingo iyi kwenikweni inapangidwira Amitundu, ndiyeno tikudziwa kuti Mulungu akufuna ife Amitundu kuti timvetse bukhu limeneli. Chaputala 2 ndi 3 cha bukhu ili chikuchita ndi mipingo isanu ndi iwiri yotchulidwa mu vesi 11.

Vesi 12: *"Ndipo ndinacheuka kuona wonena mau amene adalankhula ndi ine ndipo nditacheuka ndinaona zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolidi."*[Izi zikuonetsera kuti pamayenera kukhala mibado isanu ndi iwiri ya mpingo.]

Vesi 13: *"Ndipo pakati pa zoikapo nyalizo wina wonga Mwana wa munthu atabvala chovala chofikira ku mapazi ache, atamangirira lamba la golide pa chifuwa."*

Tsopano kodi Yohane adaona yani? Kodi iye adaona Mulungu? Iye adaona Mulungu-munthu. Inu simungathe kumuona Mulungu, koma inu mukhoza kumuona Mulungu -munthu, Yesu Khristu.

Taonani, Iye adavala chovala kufikira ku mapazi ake ndipo adzimangirira mchiuno mwake ndi lamba wachitsulo. Izi zikutanthauza kuti Iye ndi Wansembe Wankulu. Iye wavala mwinjiro wa Wansembe Wankulu. Izi ndi zakanthawi chabe, Iye sadzavala nthawi zonse monga choncho, chifukwa Iye akubweranso ngati mkwati mu maonekedwe a Mngelo Wankulu wa ku Chivumbulutso, chaputala 10 ndipo wavala mtambo, ndipo ndi mkwatibwi yekha amene akumuona mumaonekedwe awa ndipo ndi mwa vumbulutso. Kenako akukwatula mkwatibwi wake kuchoka pa dziko ngati mkazi wake. Kenako akubwera ngati mfumu pa kavalo woyera ndipo Iye adzavala chovala chovikidwa mu mwazi. [Chivumbulutso 19] Yesu *akusintha zovala* pamene ntchito zake zikusintha. Iye akusintha ma udindo pamene ntchito yake ikusintha, koma Mulungu akukhalabe nthawi zonse Wamuyaya, wosasintha.

Vesi 14: *"Ndipo tsitsi la pa mutu pache linali loyera ngati chipale chofewa; ndi maso ache ngati lawi la moto;"* [Yohane adamuona Iye monga m'mene Danieli adamuonera Iye. Izi zikuimirira Oweruza.]

Vesi 15: *"Ndi mapazi ache ngati mkuwa wonyezimira, ngati woyengeka m'nganjo ndi mau ache ngati mkokomo wa madzi ambiri."*

Mapazi ache ngati mkuwa zikutanthauza kuti Iye anaima pa chiweruzo cha inu. Zikutanthauza kuti Iye anaima pa chiweruzo, kotero, inu simukuyenera kulowa mu chiweruzo cha kutsutsidwa. Mwana wa Mulungu yemweyo, amene ali ndi moyo wa Mulungu mwa iye, anabwera ndikupereka dipo la machimo anu.

Vesi 16: *"Ndipo m'dzanja lache lamanja munali nyenyezi zisanu ndi ziwiri, ndi mkamwa mwake mudatuluka lupanga lakuthwa konse konse; ndipo nkhope yake ngati dzuwa lowala mu mphamvu yache."*

Nyenyezi zisanu ndi ziwiri mu dzanja lache lamanja zikuonetsera amithenga asanu ndi awiri a mibado ya mpingo. Lupanga la kuthwa konse konse unali uthenga wochokera kwa Khristu umene amithenga anali nawo mu tsiku lawo. Apa pali munthu wankhope yache yowala ngati dzuwa. Izi zikuonetsera Yesu Khristu, Mulungu-munthu, osati Mzimu Wamuyaya. Khristu akuonetsedweranso pa Chivumbulutso, chaputala 10 ndi nkhope yake yowala ngati dzuwa.

Vesi 17: *"Ndipo pamene ndidamuona Iye, ndinagwa pa mapazi ache ngati wakufa; ndipo anaika dzanja lache lamanja pa ine, nati, usaope, Ine ndine woyamba ndi wotsiriza."*

Yohane kugwa pa mapazi ache ngati wakufa akupereka choimirira chabwino kwa aliyense amene apeza vumbulutso la Yesu kuti ali kwekweni yani, kufa kwa iye yekha.

Vesi 18: *"Ine ndiri wamoyo, ndipo ndinali wakufa, ndipo taona, ndiri wamoyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo ndiri nazo zofungulira za imfa ndi Hade."*

Tsopano Mulungu sangafe, ndipo Iye sanakhalepo wakufa. Uyu amene amalankhula ndi Yohane, anali wakufa, koma wadzuka kwa kufa, ndipo adali tsopano wamoyo.

Uwu unali uthenga wa mu mpingo woyamba. Iwo umapita ndikumanena, "Iye wauka." Baibulo likuti ndi mphamvu yaikulu anapatsa atumwi umboni wa chiukitsiro cha Yesu Khristu. Iye anali amene ali ndi moyo, ndipo anali wakufa, ndipo anali atabweranso. Inde, Mulungu anamulora Iye kufa. Chifukwa chiyani? Chifukwa cha inu ndi ine. Iye sadzafanso, ndipo chifukwa kuti anafa, ife sitifa mwauzimu.

Gawo lotsiriza la vesi limeneli likuti, *"ndipo ndiri nazo zofungulira za imfa ndi Hade."* Yesu Khristu anapita pansi ndikukalalikira mizimu imene inali ku ndende [1Petro 3:19] Ndende inali yotsekedwa ndipo satana anali ndi zifungulo pambali pake. Izi zili ku Masalimo 24:7-10, kumene akuti, *"Weramitsani mitu yanu, zipata inu; ndipo kwezani inu; zitseko zosatha kuti mfumu ya ulemelero ilowe."* Ndipo liu linachokera pomwepo linapfuula, *"Mfumu imeneyi ya ulemelero ndani?"* Yesu anayankha nati, *"Ambuye wolimba kunkhondo."* Zipata zinatsegulidwa ndipo Iye analowa ndikutenga zifungulo zomwe zinali mbali ya satana. Iye anatsegula zipata ndikulora Abrahamu ndi enawo kutuluka. [Mateyu 27:52-53] Ndipo pamene Iye anabwerera, Iye anamupatsa Petro zifungulo. Ndicho chifukwa chache ndikofunika kubatiza monga Petro anabatizira ku Machitidwe 2:38.

Pa tsiku la Pentekosite, Petro anatsegula chitseko ku mpingo wa chiyuda ku Machitidwe, chaputala 2. Kenako iye anatsegula chitseko kwa Amitundu, kuwabatiza iwo njira yomweyo, monga anachitira ndi Ayuda pa tsiku la Pentekosite zaka zoyambirira. Tsopano Ambuye ali nazo zifungulo zochepa zosungidwira ku mpingo mu nthawi ino imene akupereka ku Utumiki Wake.

Vesi 19: *"Chifukwa chache lembera zimene uziona, ndi zimene zilipo, ndi zimene zidzaoneka m'tsogolomo."*

Mu bukhu la Chivumbulutso muli zinthu zimene zachitika kale, zinthu zimene zikuchitika ndi zinthu zimene zidzachitika m'tsogolomo. Chifukwa Yohane anamvera pa kulemba zimene anaziona, ife tikuwerenga izi ndi kuzimasulira kwa inu.

Vesi 20: *"Chinsinsi cha nyenyezi zisanu ndi ziwiri zimene unaziona pa dzanja la manja, ndi zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide. Nyenyezi zisanu ndi ziwiri ndizo angelo amipingo isanu ndi iwiri, ndipo zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri ndizo mipingo isanu ndi iwiri."*

Vesi ili likudzifotokoza lokha ndipo likutithandiza ife kuti tifotokoze vesi 4. Mu vesi 4, Yohane akulembera kwa mipingo isanu ndi iwiri ku Asia. Mosakaika, Yohane anali atalalikira ku mipingo isanu ndi iwiri imene amalembera. Yohane amalembera kwa azibusa a mipingo iyi isanu ndi iwiri. Iye amawadziwa iwo maso ndi maso, koma izi zimaimiriranso chimene chidzachitike mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo kupyola njira yonse, pamene angelo asanu ndi awiri auzimu amapereka Mau a Mulungu kwa amithenga a pansi asanu ndi awiri mu m'bado uliwonse wa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo.

Sikungoti padali wam'thenga wa pansi pano ku m'bado uliwonse pamene zimabwera ku kukwaniritsidwa, koma panali mngelo wauzimu amene amatumikira kwa amithenga a pansi pano mu uliwonse wa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Imeneyo ndiyo mizimu isanu ndi iwiri yokhala pa mpando wa chifumu mu vesi 4. Angelo amenewa akufotokozedwa bwino mu machaputala ena a mu bukhu ili. Komanso, "chinsinsi" cholankhulidwa mu vesi 20 ndi chinsinsi chomwecho chimene chikulankhulidwa pa chaputala 10 cha Chivumbulutso chimene chakwaniritsidwa ndi wam'thenga waku m'bado wa mpingo wa chisanu ndi chiwiri. Taonani mau awa **"chinsinsi"** ndi mau a chimodzi "chinsinsi" ndipo zikuyenera kukhudzana ndi mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Tipeza zambiri za izi mu chaputala 10 cha Chivumbulutso. Ku mathero, chaputala ichi chikukhudzana ndi munthu uyu Yesu Khristu kudzizindikiritsa yekha kwa Yohane. Inu mwaona onse mwana [Yesu] ndi Mulungu Atate [Mzimu wamuyaya]. Inu mwaona Mulungu akudzionetsera mu thupi kugwira ntchito zina, ndipo kotero mwaona kuti Mulungu akukhalabe Mzimu wopezeka paliponse nthawi yomweyo.Ambuye akudalitseni ndi kukupatsani inu chidziwitso
chathunthu. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHIWIRI

Chaputala 2 ndi chaputala 3 cha Chivumbulutso chikufotokoza za nyengo ya nthawi imene ikutchedwa "Ufumu wakumwamba" kapena "chinsinsi cha Mulungu," monga zalembedwa ku Mateyu 13 ndi ku Chivumbulutso 10:7 motsatana, imene ndi mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Nyengo iyi ya nthawi, gawo lake lalikulu, lakwaniritsidwa. Ife tsopano tikukhala ku mapeto kwenikweni kwa m'bado wa mpingo wa Laodikaya, ndipo mkwatibwi Oyera mtima akukhala kunja kwa iwo ngakhale pano.

Ine ndikufuna ndiike chidziwitso chapadera pa ku kuika ndemanga yomveka pa za mafanizo a pa Mateyu, chaputala 13 ndi kukulira limodzi kwa tirigu ndi nansongole zimene zikuonetsera mpingo pamene udakhala ukudutsa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Mpingo utagwa ku chiyero cha ku kumayambiro apa chiyambi, unadutsa mu nyengo ya nthawi yodziwika ndi m'bado wa Ufumu wa kumwamba. Iyi ndi nyengo yokhayo ya nthawi yodziwika ndi dzina limenelo. Zikuimirira dziko lapansi la chikhristu, zonse ziwiri choonadi ndi bodza, pamene zikukhala mbali ndi mbali kupyola mu nyengo ino ya nthawi. Palibe mu nthawi iliyonse imene mpingo unaloredwa kukhala mu chikhalidwe chimenechi.

Mu gawo loyambirira la mpingo, Mulungu sakanatha kulora chikhalidwe ichi chikhale, monga Machitidwe, chaputala 5 akuwonetsera kwenikweni. [Machitidwe 5:1-11] Pakuti apa tikuona mamuna ndi mkazi, otchedwa Anania ndi Safira, m'mene amayesera kubweretsa tchimo ndi chinyengo mu chiyanjano cha Oyera mtima. Nthawi yomweyo Mulungu anaonetsera njira zawo zoipa, ndipo onse awiri anagwa nafa pamaso pa gulu losonkhana, ndipo mantha anagwa pa iwo onse amene adaona izi. Izi zinali Mulungu asanalore nansongole kukulira limodzi mu munda umodzi ndi tirigu, umene unali Ufumu wakumwamba usanayambe umene umalora chikhalidwe chotero.

Kotero tirigu ndi nansongole zinaloredwa kukulira limodzi kupyola mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Koma monga mwa mafanizo a ku Mateyu chaputala 13, padzakhala kulekanitsa ku nthawi yotsiriza, zimene zikuchitika pano, ndipo pafupifupi zafika kumapeto nthawi ino. Ine sindibwereza izi pamene tikudutsa mu mibado ya mpingo ya mpingo apa, koma ine ndinaganiza zikanakhala zabwino kuzibweretseratu izo tisanayambe ulendo wathu kudutsa mu mibado isanu ndi iwiri ya mpingo. Titalankhula zimenezo, tiyamba ulendo wathu limodzi. Ngakhale, sitichita ndi mibado ya mpingo mopitirira, ife tikufuna kubweretsa zochuluka kulora akhristu odzipereka odzazidwa ndi Mzimu Woyera awone chimene chachitika kuyambira pa tsiku la Pentekosite mpakana pano, ndi chimene chalonjezedwa mu nthawi ino.

M'bado wa Aefeso 53-170

Vesi 1: *"Kwa mngelo wa mpingo wa Efeso lemba; izi anena Iye amene agwira nyenyezi zisanu ndi ziwiri m'dzanja lake lamanja, Iye amene ayenda pakati pa zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide."*

Yesu Khristu, yemweyo amene anazindikirika ku Chivumbulutso chaputala choyamba, akuzindikirika pa kutsegula m'bado wa mpingo uwu. M'bado wa mpingo uwu unayamba pafupifupi 53A.D. ndi kutha pafupifupi 170A.D.

Wam'thenga woyamba wapansi pano ku m'bado wa Aefeso anali Mtumwi Paulo. Ena akhoza kufunsa izi chifukwa Paulo anali atapereka kale moyo wake chifukwa cha uthenga pa nthawi imene Yohane amalemba mu 96A.D; koma kumbukirani, m'bado unayamba pafupifupi 53A.D; Paulo adakali ndi moyo. Kwenikweni, Paulo anayamba mpingo ku Efeso, ndipo mipingo ina isanu ndi umodzi yaku Asia inayamba chifukwa cha chitsitsimutso cha moto ku Efeso, koma ife sitikhudzana nazo zambiri za mpingo wa Efeso. Kotero, ine ndikufuna muone wam'thenga ndi nthawi imene mpingo unayamba. Izi ndi zofunika kuti mumvetse chinthu chotsatira chimene ndikufuna ndibweretse pa nthawi ino.

Onetsetsani kwambiri tsopano pamene vumbulutso ili likumasuka. Mpingo wa chiyuda unayamba pa tsiku la Pentekosite mu 33A.D. [Machitidwe 2], koma Paulo sanayambe mpingo wa Amitundu wa Aefeso mpakana pamene Amitundu anayamba kulandira mphatso ya Mzimu Woyera [Pentekosite wathu-Machitidwe, chaputala 10].

Pamene Paulo anayamba kutumikira Mau a moyo, iye sanali mu m'bado wa mpingo wa Aefeso, chifukwa m'bado wa Aefeso unali usanayambe. Chimene Mulungu anachita pa Pentekosite [kuyambira mu 33A.D.] kunali kuitana anthu kuchokera ku pfuko la chiyuda kupanga gawo loyamba la Mpingo Wake Woona nansongole asanalowemo. Izi zikulumikizana ndi maziko khumi ndi awiri a khoma la mzinda wa Yerusalemu Watsopano, mzinda umene ndi Mpingo woomboledwa, oyeramtima wa mafuko onse. Paulo anapita koyamba kwa Ayuda monga atumwi ena khumi ndi awiri, koma uthenga wa Paulo sunakhazikike bwinobwino kwa Ayuda, monga Mulungu pa nthawi iyi anali nawo, kapena anali mu dongosolo lotenga, anthu a chiyuda ochuluka kuwatulutsa mu pfuko kuti akakwaniritse cholinga chake.

Paulo analalikira mu nthawi yomweyo imene Mulungu amachita kwenikweni ndi Israeli, ndipo pamene Paulo amalalikira kwa Ayuda, iye adaona Mulungu akutseka chitseko ku gawo limenelo la mpingo wake kupereka chipulumutso kwa Ayuda.Iye adaona Mulungu akuchita chinthu chatsopano ku dziko. [Machitidwe 13:46-49] Paulo anali mtumwi amene Mulungu anapereka kwa Amitundu [Aroma 11:13], ndipo iye anazimvetsa bwino izi. Choncho pamene Ayuda anakana uthenga wake, iye anapita kwa Amitundu.

Ine kwenikweni ndikufuna muone apa kuti Paulo anatumikira mu gawo la nthawi iyi kuyambira 33A.D. mpakana 53A.D. Iye adamuona Mulungu akutseka chitseko ku kanyengo kochepa ka nthawi yochepa mibado ya mpingo isanayambe mu 53A.D. Paulo adaona Mulungu akutsegula chitseko ku m'bado wa ku ufumu wa kumwamba, nyengo ya nthawi imene Mulungu analora tirigu ndi nansongole kukulira limodzi, mpakana iye atabweranso ku dziko m'maonekedwe a mngelo, ku Chivumbulutso chaputala 10, kudzalekanitsa nansongole ndi tirigu ndi kudzafikitsa mkwatibwi ku ungwiro.

Inde, Paulo adaona chitseko chimodzi chikutsekeka, cha kulalikira kwenikweni kwa Ayuda, ndipo chitseko china chotseguka, cha kulalikira kwenikweni kwa Amitundu ndikulora nansongole kukulira limodzi ndi oyera mtima woona. Iyi ndi Mibado isanu ndi iwiri ya Mpingo. Poti Paulo anali mtumwi kutumikira pamene mibado ya mpingo inatsegulidwa, iye anakhala nyenyezi ya m'bado wa Aefeso, Mulungu asanamuitane kumudzi mu zaka za 66 mpakana 68; kusiyana kwa zaka ziwiri mu mbiri.

Choncho mtumwi Paulo anakhala mngelo wa m'bado woyamba ndipo iye anaika maziko a kachisi wauzimu wa Mulungu, amene ndi Oyera mtima mkwatibwi Wake.

Vesi 2: *"Ndidziwa ntchito zako, ndi chilemetso chako ndi chipiriro chako, ndi kuti sukhoza kulora oyipa, ndipo unayesa iwo amene adzitcha okha atumwi, nuwapeza onama."*

Uwu ndi m'bado wa mpingo wokhawo kumene zalembedwa kwa mngelo kuti "*ndipo unayesa iwo amene adzitcha okha atumwi, nuwapeza onama."* Ku mayambiriro a mpingo woyambawu, Mulungu

anali ndi mtumwi ndipo tikubweranso ku masiku otsiriza, pamene Mulungu adzachitanso ndi kuikanso utumiki usanu. Padzakhala nthawi imene Mulungu adzakhala ndi utumiki ngati womwewu umene udzakhala ndi utsogoleri wa Ambuye.

Mpingo weniweni unayamba ndi utsogoleri wa atumwi ndi mphamvu ya Mulungu mwa iwo, ndipo sadzayanjana ndi chilichonse chosiyana ndi chimenecho mu tsiku lino. Atumwi amalemekezedwa mu tsiku limenelo. Lero, ngati mutati ndinu mtumwi, anthu amafuna kuseka ndikumakupangani choseketsa, koma zimenezo sizingasinthe Mau a Mulungu. Mau a Mulungu adakali wolondola ndipo akuti *"Ndipo anapatsa ena akhale atumwi, ndi ena, aneneri, ndi ena alaliki, ndi ena abusa ndi ena aphunzitsi;"* [Aefeso 4:11] Utumiki usanu udakali wolondola. Lingaliro la munthu silimasintha Mau a Mulungu. Mulungu akuyenda mu nthawi ino mu njira ya pamwamba.

Tithokoze Mulungu chifukwa cha anthu amene adzayesa iwo amene akuti ali atumwi. Mu nthawi ino tikhoza kufunsa, "Tingawayese bwanji iwo amene akuti ndi atumwi?" Chingakhale cholakwika ndi chiyani ndi ife kuyeza uthenga wathu ndi uthenga wa Paulo woyera? Iye anabweretsa Mau a Mulungu, ndiye pamene ife tiyamba kulankhula za thupi limodzi, chikhulupiliro chimodzi, Ambuye m'modzi, mphatso zisanu ndi zinai za mzimu kugwira ntchito mu mpingo, mpingo wokhala ndi chikondi cha Mulungu, onse kulankhula zofanana, ndi ubatizo wa m'madzi mu dzina la Yesu Khristu, kenako mukhoza kunena " Ndi chiphunzitso cha atumwi."

Tsopano, udindo wa utumwi umene waikidwanso mu Mpingo mu tsiku lotsiriza ili ukuyenera kukhala mu mzere ndi Baibulo, chifukwa chilichonse chimene sichili mu mzere ndi Baibulo, ife sitingathe kuchivomereza. Paulo anati iye anaika maziko ku mpingo, ndipo maziko amenewo ndi zolemba za Paulo Woyera, pamene iye anatenga zimene atumwi ndi aneneri a m'mbuyo mwake ananena za dongosolo la Mulungu.

Baibulo likuti adawayesa iwo amene amati ndi atumwi ndikuwapeza onama. Adawayesa iwo motani? Iwo amafufuza zimene zimalankhulidwa ndi zimene Paulo anaphunzitsa ndi kupeza kuti sizinali mu mzere wolondola. Choncho iwo anali onama.

Vesi 3: *"Ndipo uli nacho chipiriro ndipo walora chifukwa cha dzina langa osalema."*

Tithokoze Mulungu chifukwa cha mpingo ngati umenewu. Anali ndi chipiriro ndipo analora chifukwa cha dzina lake wosalema ngakhale dzina la m'bado limaonetsa mtundu wa mzimu umene umayenera kugonjetsa. Mau oti "Efeso" ali ndi tanthauzo monga *kulekerera ndi kuchoka.* Iwo analekerera ku moto [koma osati onse] umene Paulo Woyera adali nawo pamene mphamvu ya Mulungu Wamoyo idali pa iwo. Iwo adalekerera ndiye kenako anayamba kuchoka, koma Mulungu anatumiza uthenga kuwadzudzula iwo ndi kuyesera kuwaitana kubwereranso ku Mau a Mulungu, kubwereranso ku chiyambi. Komabe, Iye adawayamikira iwo, iwo amene anakhala woona, chifukwa anagwira ntchito ndipo sanalema, ndipo amadziwa m'mene angawayesere iwo amene amati anali atumwi.

Vesi 4: *"Koma ndiri nako kanthu kotsutsana ndi iwe, kuti unataya chikondi chako choyamba."*

Tikuyenera kusamalitsa kuti mwina chinthu chomwecho chibwera pa ife chimene chinabwera pa m'bado wa mpingo woyamba. Ife tikukhala mu nthawi imene Mateyu 24:12 akuti, *"Ndipo chifukwa cha kuchuluka kwa kusayeruzika, chikondano cha anthu aunyinji chidzazirara."* Ife tikukhala mu chikhalidwe chomwecho, chikhalidwe cha Laodikaya, ndipo pamene chikondi cha Mulungu chikuzirara pakati pa Oyera mtima ena tiyeni tikhale openyetsetsa nthawi ili yonse.

Vesi 5: *"Potero kumbukira kumene wagwerako, nulape, nuchite ntchito zoyamba; koma ngati sutero, ndidzadza kwa iwe, ndipo ndidzachotsa choikapo nyali chako, kuchichotsa pamalo pake, ngati sulapa."*

Mu 96A.D. mpingo uwu umene unali utayambika ndi Paulo unali utagwa kale, monga zafotokozedwa momveka mu vesi 5. Khristu anati, Iye adzachotsa choikapo nyali, pokhapokha m'bado uwu ulape.

Palibe m'bado umene unapanga kubwerera utagwa kuchokera ku chitsitsimutso cha pa chiyambi chimene chinayambitsa m'bado umenewo. Kusuntha kwa choikapo nyali kunachitika mu 170A.D. ndipo Mulungu anayatsa choikapo nyali china ku m'bado otsatira.

Vesi 6: *"Koma ichi uli nacho kuti udana nazo ntchito za Anikolai, zimene inenso ndidana nazo."*

Tayang'anani: zochita za a Nikolai. Mau oti "Chinikolai" akuchokera ku mau a chigiriki, "Nikao" amene amatanthauza *kugonjetsa,* ndipo "Laos," amene amatanthauza *anthu wamba.* Izi zimatanthauza kugonjetsa anthu wamba kapena kuchotsa chili chonse kwa anthu wamba ndi kuziika kwa wansembe. Tiyeni ife tisagwe mu msampha omwewo mpingo uwu unagweramo pamene iwo anakhwimitsa magome ndikubereka kachitidwe ka Chinikolai.

Ma Edala a ku Efeso anatenga mphamvu zochuluka kwa anthu wamba kuti pasachitike china chilichonse iwo osadziwa, ngakhale Mzimu wa Mulungu. Mulungu akufuna kuyenda mu thupi ndi malilime ndi uneneri, ndi mamasulidwe, ndi ulemerero wa Ambuye kudalitsa Oyera mtima. Machitidwe a Chinikolai analowa mu mpingo ndipo Mulungu anati Iye amadana nazo, ndipo Iye sanasinthe malingaliro Ake. Iye amadana nawobe machitidwe a Chinikolai pamene munthu wina ayesera kuwamanga anthu wamba. Mulungu adzakhala nawo Mpingo umene udzayenda ndi mphatso za Mzimu monga unachitira mu masiku a Paulo Woyera. Pali ufulu wa ana a Mulungu.

Vesi 7: *"Iye wokhala nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa mipingo. Kwa Iye amene alakika ndidzampatsa kudya za mtengo wa moyo umene uli m'paradaiso wa Mulungu."*

Tayang'anani, amayenera kukhala ndi khutu la uzimu kuti amve uthenga umene ukanawapatsa iwo moyo osatha, ndipo mu m'bado uli wonse wa mpingo pali anthu amene amadya za mtengo wa moyo. Ili ndi lonjezo kwa ogonjetsa a mu m'bado umenewo. Kachiwirinso, m'bado uwu wa Aefeso unatenga nthawi yoyambira 53A.D. mpaka 170A.D.

M'bado wa Smurna 170-312

Vesi 8: *Ndipo kwa mngelo wa mpingo wa ku Smurna lemba; izi anena woyamba ndi wotsiriza, amene anakhala wakufa, nakhalanso wamoyo;"*

Chaputala choyambirira cha bukhu la Chivumbulutso chikuonetsa kuti uyu ndi Yesu. Iye anali wakufa ndipo tsopano ali ndi moyo. Iye ndi woimirira wa m'bado wakugwa uno. Iye akudzionetsera yekha mu m'bado uliwonse wa mpingo. Iye anayenda pakati pa zoikapo nyali zisanu ndi ziwiri za golide. Iye anali mu mpingo kudutsa njira yonse mpakana gawo lotsiriza, Laodikaya, pamene Iye akuikidwa kunja.

Mngelo, kapena wam'thenga wapansi pano ku m'bado wa Smurna anali Iraniasi, munthu amene anakhala woona kwa Mulungu mu tsiku lake. [Taonani: kulandira ndi kugwirizana ndi malemu William Branham pa Ireniasi kukhala wam'thenga wapampansi pano ku m'bado uwu.]

Mau oti "Smurna" amatanthauza *kuwawa*. Izi zikutiuza kuti uwu unali m'bado wa chisautso chowawa cha Oyera mtima a mu m'bado. Chirichonse chimene chimachitika mu mpingo wa mu mzinda wa Smurna chikutionetsera chimene chikanachitika mu m'bado wa Smurna, pamene nyengo ya nthawi imeneyi imafika.

Mu mzinda wa Smurna, Oyera mtima anali wosauka ndipo amakumana ndi mayesero olimba ambiri, koma tithokoze Mulungu mbewu yoona ya Mulungu inakhala moona ku uthenga umene Iraniasi ndi azitumiki ena woona analalikira.

Vesi 9: *"Ndidziwa ntchito zako, chisautso chako, ndi umphawi wako [komatu uli wa chuma], ndi mwano wa iwo akunena za iwo okha kuti ali Ayuda, osakhala Ayuda, komatu Sunagoge wa Satana."*

Uwu unali m'bado wa chisautso chachikulu ndi umphawi. Komabe anali a chuma chifukwa anali ndi vumbulutso. Ngati inu muli ndi vumbulutso la Mau a Mulungu ndiye inu ndinu wachuma mwa Mulungu.

Mutsiku limenelo, panali Ayuda ndi ma sunagoge ochuluka. Mu tsiku ili, tili ndi mipingo yopatuka yosiyana siyana ndi mipingo ya zipembedzo za chikatolika imene ndi masunagoge a satana. Komanso, izinso zikupita kwa mipingo yambiri yoima payokha imene ikuti iwo si chipembedzo [mpakana amalalikira motsutsa chipembedzo], koma akugwirabe zambiri za ziphunzitso zake [katolika wachiroma]. Kotero, izi zikukamba za m'bado wa mpingo wa chipembedzo wa Amitundu usanayambe. Kunali masunagoge a chiyuda kulikonse komwe Ayuda amakumana, koma Yohane anati iwo anali masunagoge a satana, chifukwa anali atakana Yesu Khristu mpulumutsi.

Vesi 10: *"Usaope zimene uti udzamve kuwawa; taona mdierekezi adzaponya ena a inu m'nyumba ya ndende, kuti mukayesedwe, ndipo mudzakhala nacho chisautso masiku khumi; khala wokhulupirika kufikira imfa, ndipo ndidzakupatsa iwe korona wa Moyo."*

Masiku khumi a chisautso awa amakamba za nyengo ya zaka khumi ya chisautso chachikulu. Oyera mtima a Mulungu anaphedwa ndi Aroma ochuluka zikwizikwi, koma Mulungu anawauza kuti asaope chilichonse cha zinthu izi, koma akhale okhulupirika kufikira imfa ndipo adzawapatsa korona wa moyo. Tayang'anani, Iye sanati "mpakana imfa," koma, "kufikira imfa."

Vesi 11: *"Iye wokhala nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa mipingo. Iye amene alakika sadzachitidwa choipa ndi imfa yachiwiri."*

"Imfa chachiwiri" iyi ikuonetsera kuti munthu wamkati adzafa ndikusadzaonekanso pokha pokha titatenga moyo wake wa Mulungu, umene ndi moyo wokhawo wa muyaya umene ulipo. **Ichi ndi chifukwa chake hade siwamuyaya. Wina akuyenera kukhala ndi moyo wamuyaya kuti akhale ku hade mwamuyaya,** koma imfa ndi hade yaponyedwa mu nyanja ya moto.[Chivumbulutso 20:14] Iyi ndi imfa ya moyo. Imfa yoyamba ndi imfa ya thupi. Imfa yachiwiri ndi imfa ya munthu wa mkati. Mulungu anauza m'bado uwu kuti iwo ukanatha kupha thupi, koma osati moyo. Mulungu amauza m'bado uwu kuti udzavutika ndi chisautso chachikulu. Pamene Yohane amalemba izi, ngakhale mpingo wa mu mzinda wa Smurna umadutsa mu chisautso chachikulu. Uwu unali m'bado wa ululu kwa Oyera mtima amenewo, koma iwo anagwiritsitsa mokhulupirika. Ife, nafenso, tikuyenera kuzunzika lero chifukwa cha uthenga uwu. Iwo ndi wokanidwa, koma pali gulu lodzazidwa ndi Mzimu la anthu mu nthawi ino limene likukhulupirira Mau onse a Mulungu.

M'bado wa Pergamo 312-606

Vesi 12: *"Ndipo kwa mngelo wa mpingo wa ku Pergamo lemba: Izi anena Iye wokhala nalo lupanga lakuthwa konsekonse,"*

Mpingo unakhala koyambirira 312A.D. mpaka pafupifupi 606A.D. Marteni Woyera ndi amene anali wam'thenga wa m'bado uwu wa Pergamo. **Apa ndi pamene mpingo ndi dziko zinalumikizana pamodzi, chikhristu ndi chikunja.** Uwu ndi m'bado umene chipembedzo choyamba chinayamba. Apa ndi pamene Constantine analumikiza mpingo ndi boma pamodzi ndi kupanga chikhristu chimodzi cha zipembedzo zapamwamba. Apa ndi pamene mpingo wa Hule wa Katolika wa Chiroma unayamba.

Vesi 13: *"Ndidziwa ntchito zako, ndi kumene ukhalako, ngakhale kuja kuli mpando wa chifumu wa satana; ndipo ugwira dzina langa, osakaniza chikhulupiriro changa, angakhale m'masiku a Antipa, mboni yanga, wokhulupilika wanga, amene anaphedwa pali inu, kuja akhalako satana."*

Apa pa vesi 13, Mulungu akuuza mpingo wa ku Pergamo kuti Iye akudziwa zonse za iwo, ndi zonse za ntchito zawo. Iye akuwauza iwo kuti Iye akhoza kuyang'ana mu mpingo wa Pergamo ndikuwauza iwo penipeni pamene Satana akukhala.

Mipingo isanu ndi iwiri imeneyi yaku Asia inali itayamba ndi chitsitsimutso, ndipo patapita zaka 40 satana anali atalowa kale ndikutenga mpando wake mu mpingo. Kotero, ife tikuyenera kukhala opemphera nthawi iliyonse.

Munthu uyu, Antipa, anali woyera mtima wankulu mu nthawi imeneyo, ndipo iye anaphedwa. Bwanji ena a ife tikanaphedwa? Zikanatha kukhala zophweka kuzindikira ndi maso a thupi kuti satana ndi amene wakonza, koma satana mu nthawi ino akugwira ntchito mosiyana ndi m'menemo. Iye akuyesera kutinyenga ife pogwiritsa gawo la Mau a Mulungu molakwika, **koma tithokoze Mulungu chifukwa cha utumiki woona umene umaimika pakamwa pa onyenga.** [Tito1:11]

Vesi 14: *"Komatu ndiri nazo zinthu pang'ono zotsutsana ndi iwe, popeza uli nawo komweko akugwira chiphunzitso cha Balamu, amene anaphunzitsa Balaki aponye chokhumudwitsa pa maso pa ana a Israeli, kuti adye zoperekedwa msembe kwa mafano, nachite chigololo."* Balamu anayesera kutemberera ana a Israeli, koma nthawi iliyonse anatsegula pakamwa pake dalitso limatuluka. Choncho Balamu anauza Balaki kupanga phwando lalikulu ndikutenga achinyamata a ana a Israeli ndi a chinyamata a Moabu pamodzi.

Tsopano, pamene a Moabu amapembedza, amachita mchitidwe wogonana mu nthawi yopembedza. Izi zikumveka moipa koma ndi zoona. Pamene iwo anayamba kuchita zimenezo, ana a Israeli anatenga atsikana a Chimoabu, kupanga nawo za dama, ndipo Mulungu amayenera kuwaweruza. Lero mzimu womwewo uli pano, koma ukuchita mu njira ya uzimu. Chiphunzitso chomwecho cha Balamu chinalumikiza akhristu ndi akunja palimodzi. Ndi chimene chinachitika mu 325A.D. Zinafaniziridwa mwangwiro mu Chipangano Chakale.

Konsitantine anatenga chiphunzitso cha Balamu ndi kulumikizitsa akhristu ndi akunja pamodzi, ndiye Mulungu amayenera kukana chinthu chonsecho. M'bado wa mpingo umenewo unatha ndipo m'bado wa mpingo wina unayamba chiphunzitso cha Balamu chidakalipo lero. Chikufuna ife tilumikizane ndi tiana tatikazi timahule, koma ife tisunga kusonkhana kwathu kukhale koyera.

Kusuntha kwakukulu uku kukulumikizitsa achikatolika, achibaptist, achimethodist ndi ena pamodzi koma iwo sasamala za Mau a Mulungu, sichilichonse koma chiphunzitso cha Balamu chimene akufuna. Satana akufuna kuwalumikiza iwo pamodzi ndi kuwapanga iwo kuchita za dama limodzi kuti mkwiyo wa Mulungu udzakhuthulidwe pa iwo mu nthawi ya chisautso, koma Mulungu watulutsa mkwatibwi wake chifukwa cha dzina lake mu nthawi ino.

Ine ndimakhulupirira chiyanjano, koma ine sindimakhulupirira kuyanjana ndi ziwanda. Paulo anati osati kuchita izo ku 2 Akorinto 6:17- *"Dzipatuleni ndipo ndidzakulandirani"* Ine ndikanakhoza kukhudzana motalika ndi chiphunzitso cha Balamu koma inu mukhoza kuziwerenga mu Baibulo lanu ku Numeri chaputala 23, 24, ndi 25. Zimene anachita zinali za thupi, iwo anachita m'chitidwe wogonana. Izo zikumveka moipa koma kodi mukudziwa kuti chinthu chomwecho chikuyendabe lero mu chimpwirikiti cha mipingo **mwauzimu?** Mzimu womwewo uli mu dziko lero. Mulungu akhala naye mkwatibwi ndipo iye sakhala akuchita za dama. Iye adzakhulupirira Mau, ndi chilichonse chotsutsana ndi Mau, mkwatibwi adzachisiya chokha chifukwa iye ali ndi ubatizo woona wa Mzimu Woyera. Mkwatibwi ali ndi mbewu ya Mulungu, ndipo mbewu imeneyo ya Mulungu, idzadya pokhapo pa Mau a Mulungu.

Vesi 15: *"Kotero uli nawo akugwira chiphunzitso cha Anikolai momwemonso, chimene ndidana nacho."*

Tayang'anani, mu m'bado wa mpingo woyamba ichi chinali kachitidwe ka Chinokolai. Kachitidwe, kapena kanthu kakang'ono, kamene kanayamba kuphunzitsidwa ndipo sizimaoneka zoipa kwambiri, **koma chinasandulika chiphunzitso.** Chipatso cha kachitidwe kukhala chiphunzitso zinali pamene Mpingo wa Katolika wa Chiroma unakhazikitsa Papa. Zinayambika ngati kachitidwe kakang'ono ka Chinikolai mu m'bado wa mpingo woyamba. Anaika kalamulo kakang'ono ndi kuika mlaliki pamwamba Paulo atatengedwa pa dziko, pamene **Mulungu amatanthauza kuti utumiki wake ukhale gawo la thupi.** Iye samatanthauza kuti utumiki ukhale pamwamba kuti usakhale ndi kulumikizana ndi mpingo. Iye samatanthauza kuti mtumiki akhale ngati Papa, akhale pamene inu mukhoza kuyembekezera mpaka miyezi isanu ndi umodzi kuti mulankhule naye. Mulungu samafuna kuti zikhale mu njira imeneyo. Iye

anati ku Agalatiya 6:6- *"Koma iye amene aphunzira Mau, ayenera kuchereza womphunzitsayo m'zonse zabwino."* Mpingo ndi utumiki ndi amodzi.

Mulungu anadana ndi machitidwe a Chinikolai mu m'bado woyamba ndipo Iye amadana nawo tsopano. Iye ndi Mulungu wosasinthika. Iye akufuna thupi la mamembala ambiri, monga Paulo adanenera ku 1 Akorinto, chaputala 12. **Mdierekezi akudziwa kuti ngati angalekanitse utumiki ndi anthu ndiye kuti wadula mutu ku thupi mwauzimu.**

Zipembedzo izi zimapanga ma Ovasiya, Ovasiya wankulu, ndi ma Bishopi. Ichi ndi machitidwe omwewo a Chinikolai, ndipo amachokera pa malo omwewo. Zikuchokera kwa satana. Mulungu anati Iye amadziwa pamene mpando wa satana uli; ndi mpando waukulu.

Vesi 16: *"Chifukwa chake lapa; ukapanda kutero ndidza kwa iwe posachedwa, ndipo ndidzachita nawe nkhondo ndi lupanga la m'kamwa mwanga."*

"Lupanga la mkamwa mwanga" ndi Mau a Mulungu. Mulungu anachita nkhondo ndi m'bado uwu ndipo potsiriza unalowa mu m'dima waukulu, ndipo Iye anayamba m'bado wa mpingo wina. Pamene mibado iyi imaonongeka ndikusaopa Mulungu, **Iye amayatsa nyali ina ndikuzimitsa ina ija.** Choonadi cha Mulungu chayenda kupyola mu mibado iyi kwa pafupifupi zaka zikwi ziwiri, ndi m'bado wa chinsinsi wa Chivumbulutso 10:7 ndipo zafotokozedwa kumeneko.

Vesi 17: *"Iye wakukhala nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa mipingo. Kwa iye wolakika, ndidzampatsa mana obisika ndipo ndidzampatsa mwala woyera, ndi pa mwalawo dzina latsopano lolembedwapo, wosalidziwa munthu aliyense koma iye wakuulandira."*

Mana wobisika anali Mau a Mulungu. Mwala woyera ndi vumbulutso. Ili ndi vumbulutso lanu, kapena chiyanjano, ndi Mulungu. Vumbulutso la Petro limatchedwa *mwala* pamene Yesu anamuuza iye kuti thupi ndi mwazi sizinaulure izo kwa iye. [Mateyu 16:17-19] Uku kunali kulumikizana kwa Mulungu mwa Oyera mtima a mu nthawi imeneyo, ifenso tikuyenera kukhala ndi chinthu chomwecho mu nthawi ino.

M'bado wa Tiratiya 606-1520

Vesi 18: *"Ndipo kwa mngelo wa mpingo wa ku Tiyatira lemba: Izi anena mwana wa Mulungu, wokhala nawo maso ake ngati lawi la moto, ndi mapazi ache ngati mkuwa wonyezimira."*

Kolamba, munthu wa Mulungu, anali wam'thenga wa m'bado wa Tiyatira. Zanenedwa ndi wam'thenga wa ku m'bado wa mpingo wotsiriza kuti mau oti "Tiyatira" amatanthauza *mkazi wolamulira.* Mai hule wachikulireyu amalamulira dziko. M'bado uwu unali m'bado wa Tiyatira kapena m'bado wa m'dima. M'bado uwu unayambira 606A.D. mpaka 1520A.D. Pamene upapa unaikidwa ndipo zonse zinachotsedwa kwa anthu wamba, Baibulo linatengedwa ndipo dziko linalowa mu m'dima waukulu kwa zaka chikwi. Iyi inali mileniamu ya satana. Ena mu mpingo wa Katolika akukhulupirira kuti mileniamu inayamba nthawi yomweyo. Wotsutsakhristu ndi mkazi wake analamulira dziko kwa zaka chikwi. Panali umphawi waukulu ndi matenda. Tchimo linakula mu m'bado uwu. Anali satana ndi mkazi wake kulamulira dziko kwa zaka chikwi. Mtsogolomu Yesu ndi mkazi wake adzalamulira kwa zaka zikwi. Mu m'bado umene satana analamulira, munali umbuli, umphawi, matenda, kupha, milili, ndi kupusa. Zimakhala ngati dziko linabwerera mbuyo, zikuoneka ngati, kwa zaka chikwi, koma pamene Khristu ndi mkazi wake alamulira padzakhala chitukuko, chisangalalo, chimwemwe, ndipo ngakhale zipululu zidzaphuka. [Yesaya 35:1]

Vesi 19: *"Ndidziwa ntchito zako, ndi chikondi, ndi chikhulupiriro, ndi utumiki, ndi chipiriro chako, ndi kuti ntchito zako zotsiriza zichuluka kuposa zoyambazo."*

Oyera mtima anavutika mu nthawi imeneyo, zonse chifukwa cha Yesu, zonse chifukwa cha Mau a Mulungu ndi chikondi pa Mulungu. **Oyera mtima amenewo anali ndi malawi a moto akuyaka m'mitima mwawo, ndipo kuphedwa komanso kulekanitsidwa wina ndi mzake sikukanatha**

kuzimitsa. Iwo amapembedza Mulungu mu mapanga, kapena paliponse pamene amapeza mwai. Lero tili ndi nyumba zabwino, karipeti paliponse, zotenthetsa nyumba, zoziziritsa nyumba koma anthu sakufuna kubwera ndi kuzapembedza Mulungu. Ife tingaime nawo bwanji Oyera mtima amenewo?

Vesi 20*: "Komatu ndiri nako kotsutsana ndi iwe, kuti ulola mkazi Yezebeli, wodzitcha yekha mneneri; ndipo aphunzitsa, nasokeretsa akapolo anga, kuti achite chigololo ndi kudya zoperekedwa nsembe kwa mafano."*

Izi zinalembedwa ku mpingo uwu ku Tiyatira. Zanenedwa kuti panali mkazi wotchedwa Yezebeli mu mpingo umenewo ku Tiyatira mu masiku amene Yohane amalemba kalata imeneyi. Ena mwa azitumiki obwerera mbuyo aku Tiyatira amachita naye chigololo, koma zikuimiriranso nyengo imene idzakhalepo mu m'bado wa Tiyatira. Iwo anachita chigololo ndi mzimu wa otsutsakhristu umene unabwera mu mpingo.

Pa nthawi iyi mu mbiri, mpingo wa ku Roma unali ndi mphamvu zambiri mpakana umaphunzitsa akapolo a Mulungu. Pamene m'bado wina unafika, Marteni Lutera amaphunzitsidwa ndi iye, iye pokhala mtumiki weniweni wa Mulungu, koma tsono Mzimu wa Kukonzanso unayamba kubwera pa iye ndipo anapatsa Roma chibala chachikulu mwa lupanga la Mzimu ndipo Kukonzanso kunayambika!

Vesi 21: *"Ndipo ndampatsa iye nthawi kuti alape; koma safuna kulapa kusiyana nacho chigololo chake."*

Mulungu anati anamupatsa iye nthawi kuti alape koma sanalape. **Mulungu anapereka nthawi ku mpingo wa Katolika kuti ulape mu M'bado wa M'dima.** Iye sanalape nthawi imeneyo, ndipo sadzalapanso. Iye adzadzuka ndikuphanso, chifukwa kupha kudakali mu mtima wake wosalapa. Mulungu anamupatsa iye kulapa kupyolera mu uthenga wa Kolamba ndi amuna ena a munthawi imeneyo amene anali odzozedwa ndi Mulungu, kuyesera kuwaitanira ku Mau, koma sanazimvere, Mulungu anati tsiku lake lapita. Kenako Mulungu anayamba kupereka mpata kwa ana ake akazi kuti alape, ndipo iwo, monga mai wao, sadzalapa ndi kusiya zipembedzo zawo.

Vesi 22: *"Taona ndidzamponya iye pakama, ndi iwo akuchita chigololo naye kuwalonga m'chisautso chachikulu, ngati salapa iwo ndikuleka ntchito zache."*

Izi zimapitirira, ngakhale kudutsa mu m'bado, mpakana mu nthawi imene Mulungu adzaponya mpingo wa Katolika wa Chiroma ndi onse ana ake akazi otsutsa mu chisautso, chifukwa palibe aliyense wa iwo amene adzalapa.

Vesi 23: *"Ndipo ndidzaononga ana ache ndi imfa; ndipo idzazindikira mipingo yonse kuti ine ndine Iye amene ayesa imso ndi mitima; ndipo ndidzaninkha kwa yense wa inu monga mwa ntchito zanu."*

Ulosi uwu pa ana akazi mu chisautso unali wa muyeso wautali. Ukudutsa mopitirira m'bado wa mpingo uwu, chifukwa ukukamba za ana akazi. Mwana wa mkazi otsiriza kubadwa mwa hule uyu ndi mwana wa mkazi wa chipentekosite. Kusuntha kwakukulu kotsiriza kunali kusuntha kwa chipentekosite. Ana akazi onsewa anabadwa mu uhule. Ndiye apo pakubwera mipingo yoima payokha, ndipo ikugwera mu mzere umodzi ndi iwo.

Vesi 24: *"Koma ndinena kwa inu, kwa otsala a ku Tiyatira, onse amene alibe chiphunzitso ichi, amene sazindikira zakuya za satana, monga anena, Sindikusanjikizani katundu wina."*

Vesi 24 ikupita koyamba kwa wam'thenga wa m'bado. *"Koma kwa inu"* ndi kwa wam'thenga; *"kwa otsara a ku Tiyatira"* ndi mpingo weniweni wa nthawi imeneyo.

Yesu Wansembe Wankulu akuyendabe pakati pa zoikapo nyali kutsimikizira mpingo kuti ngakhale m'dima uchuluke motani, Iye adakali nawo kuthandizana nawo pa chipsyinjo ndi kupereka mphotho chifukwa chokaniza satana.

Vesi 25: *"Koma chimene muli nacho, gwirani kufikira ndikadza."*

Vesi 26: *"Ndipo iye amene alakika, ndi iye amene asunga ntchito zanga kufikira chitsiriziro, kwa iye ndidzampatsa ulamuliro wa pa Amitundu."*

Lonjezo limene Mulungu anapereka kwa ogonjetsa a ku m'bado uwu silikanatha kukwanira bwino. Hule anali atalamulira kwa zaka chikwi, ndipo Yesu anauza m'bado uwu kuti ngati atagonjetsa Iye akanawalora iwo kulamulira kwa zaka chikwi ndi Iye.

Vesi 27: *"Ndipo adzawalamulira ndi ndodo ya chitsulo, monga zotengera za woumba mbiya ziphwanyika ndi mapale; monga Inenso ndilandira kwa Atate wanga."*

Mulungu anapanga lonjezo ili kwa ogonjetsa a ku m'bado wa Tiyatira, chifukwa iwo anali amene amayenera kukhala mu m'bado umenewo. Inde, Oyeramtima awa amayenera kukhala mu m'bado umene mpingo wa mdierekezi umalamulira ndi ndodo ya chitsulo. Kotero Mulungu akuwauza iwo kuti adzakhala ndi ulamuliro kulamulira ndi Iye mu Mileniamu. Ife sitinaone zimene iwo anaziona. Ife tikhoza kuwerenga mbiri, koma iwo amayenera kukhala ndi moyo kupyola mu zimenezo. Iwo amakhala pomwepo pamene satana amalamulira. Ngakhale satana analamulira, Mulungu anali nawo ogonjetsa mu m'bado umenewo.

Vesi 28: *"Ndipo ndidzampatsa iye nthanda."* [Yesu ndiye nthanda. [Chivumbulutso 22:16] Ndipo kulandira Yesu ndikulandira Moyo Wosatha.]

Vesi 29: *"Iye wokhala nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa mipingo."*

Vesi 29 likuonetsa kuti zimatengera vumbulutso mu m'bado uli wonse kugwira uthenga wa mu nthawi. Panali uthenga mu m'bado wa mpingo uli wonse kwa anthu wodziwidwiratu kuti amve. Zikomo Mulungu chifukwa cholankhula ndi mpingo wake ngakhale mu nthawi ya m'dima. Amen.

CHIVUMBULUTSO CHAPUTALA CHACHITATU

M'bado wa Sarde 1520-1750

Mizimu isanu ndi iwiri mu vesi loyambirira ndi angelo auzimu asanu ndi awiri amene akuoneka ku Chivumbulutso 1:4. Nyenyezi zisanu ndi ziwiri ndi amithenga asanu ndi awiri apansi pano ku mibado ya mpingo isanu ndi iwiri. Chonde yang'anani izi pamene tiwerenga vesi loyamba.

Vesi 1: *"Ndipo kwa mngelo wa Mpingo wa ku Sarde lemba: Izi anena Iye wakukhala nayo mizimu isanu ndi iwiri ya Mulungu, ndi nyenyezi zisanu ndi ziwiri; ndidziwa ntchito zako, kuti uli nalo dzina lakuti uli ndi moyo, ndipo uli wakufa."*

Pamene anena kuti, *"kwa mngelo"* zikutanthauza kuti mngelo wachisanu wauzimu anali ndi udindo wotenga vumbulutso kwa oyeramtima a mu m'bado umenewo, osati kwa munthuyo [wam'thenga wapansipano], koma mngelo wa uzimu amakhudza m'bado onse. Kotero vesi loyamba ndi kwa mngelo wa uzimu ndi kwa munthu.

Dzina loti "Sarde" limatanthauza *othawa.* Marteni Lutera anali wam'thenga wapansipano wa mu m'bado uwu wa othawa. Lutera anali ndi chitsitsimutso chachikulu. Mphamvu ya Mulungu inali mu mpingo, Mulungu anapereka chiombolo chachikulu, ndipo anathawa.

Kuchokera pafupifupi 1200A.D. kumapita, anthu anayamba kumayesera kumathawa kutuluka mu mpingo wa Katolika wa Chiroma. Iwo sakanatha chifukwa mpingo wa Katolika wa Chiroma umatumiza ankhondo ndi kumawapha zikwi zikwi, <u>koma pamene nthawi ya Mulungu inafika ya Kukonzanso, panalibe chimene chikanaletsa.</u>

Wophunzira wotchedwa Marteni Lutera, amene anaphunzira ndi kudziwa katekisimu, koma samapeza mtendere ndi Mulungu, anawerenga Baibulo pamene linati *"Olungama adzakhala ndi moyo mwa chikhulupiriro."* <u>Mawu amenewa amangooneka ngati akukwera kuchoka pa tsamba</u>. Iye anayamba kulalikira kuti sumayenera kukhala ndi moyo mwa zolankhula za papa, koma kuti mukhale ndi moyo mwa zolankhula za Yesu.

Lutera analemba mfundo 95 zotsutsana ndi mpingo wa chikatolika wa Chiroma ndikukhoma pa chitseko cha tchalitchi [kasitolo] pa 31 Okotobala, 1517. Ichi chinafotokoza chimene anali nacho

chotsutsa Katolika wa Chiroma. Pamene iye amalalikira mochuluka Mau a Mulungu, mochuluka anthu amapita ku Mau. Mosakhalitsa Germany anayaka nacho chitsitsimutso. Pamene Germany amayaka ndi chitsitsimutso, anthu ambiri anachuluka ndi kukhulupirira chimene Lutera analankhula.

Lutera anapambana pa kutulutsa anthu, koma chinthu chokhumudwitsa pa m'bado uwu ndi chakuti moto wa chitsitsimutso unafa mwansanga ndipo amangokhala mwa mbiri ya chimene anali pa chiyambi pa m'bado. Yesu anati, *"Uli nalo dzina lakuti uli ndi moyo, ndipo uli wakufa."* Koma moyo wa Mulungu unakhala mu m'bado umenewu kwa nthawi yaitali kutumikira cholinga cha Mulungu. Kenako moyo wa Mulungu unasunthira ku Mau ake.

Vesi 2: *"Khala wodikira, ndipo limbitsa zotsalira, zimene zinafuna kufa; pakuti sindinapeza ntchito zako zakufikira pa maso pa Mulungu wanga."*

Izi zinali za ku mpingo mu mzinda wa Sarde, umene unali mu nyengo imene ikanafanana ndi m'bado wa Sarde mu 1500A.D.

M' bado wa Sarde unalibe zambiri, kulapa kokha. Anthu awa anayamba kuchoka, koma mzimu wa chipembedzo unayamba kuonekanso, mai hule uyu anayamba kukhala ndi ana akazi. Iye anachita chigololo ndipo anali nawo ana. Iwo sanabadwe mwa Mau a Mulungu.

Vesi 3: *"Chifukwa chache kumbukira umo unalandira nunamvamo; nusunge nulape. Ukapanda kudikira tsono, ndidzafika ngati mbala, ndipo sudzazindikira nthawi yache ndidzadza pa iwe."*

Yesu anauza mpingo uwu kuti akumbukire zimene unalandira ndi kumva. Zimene mumamva zimatanthauza zambiri. Mulungu amadziwa kuti zikanatanthauza chinachake mu m'bado uwunso. Kotero Mulungu anatumiza mngelo uyu ndi uthenga, ndipo Lutera anayamba kuulalikira mu m'bado wa mpingo uwu. Iye anawauza iwo kuti "agwiritse ndi kulapa." Iwo anauzidwa kugwiritsa choonadi cha Mau a Mulungu a mu tsiku limenelo. Iwo amayenera kulapa za zintchito zawo zolakwika ndi zolephera zawo. Mulungu akufuna mpingo uchite chomwecho lero.

Kotsalira kwa vesi 3 likuti, *"Ukapanda kudikira tsono, ndidzafika ngati mbala, ndipo sudzazindikira nthawi ndidzadza pa iwe."* Ili ndi chenjezo lenileni. **Mulungu anabwera ku mapeto kwa m'bado wa mpingo uwu ndi choonadi chambiri, ndipo iwo anagwidwa amaliseche. Iwo sakanatha kupitirira ndi Mulungu. Mulungu amayenera kuyatsa nyali ina ndikuzimitsa ija.** Nyali zimenezo zimayatsidwa koma zimayaka mwa kanthawi.

Mulungu anauza m'bado wa Aefeso kuti ngati sulapa Iye akanabwera ndi kusuntha choikapo nyali, kutanthauza "kuwala" kunasunthidwa kupita ku m'bado wina. Ku Chivumbulutso, chaputala 4 nyali zonse zisanu ndi ziwiri zikuyaka pa mpando wa chifumu wa Mulungu, kusonyeza kuti nyali imayatsidwa mu m'bado uli wonse wa mibado isanu ndi iwiri ya mpingo ndipo yatha. [Chivumbulutso 2:5] Choikapo nyali chimachotsedwa pamene m'bado uliwonse umapita kumapeto. Mulungu anayatsa nyali ya Yohane Wesile mu 1750, ndipo Iye anazima nyali ya Lutera, ndipo yakhala yozima nthawi yonse. Mulungu sangapitenso ku m'bado wa mpingo umenewo. Iye amangopitirira ku m'bado wina mpakana m'bado wachisanu ndi chiwiri ndipo kenako zimakwanira m'bado yonse ya mpingo.

Vesi 4: *"Komatu uli nao maina owerengeka m'Sarde; amene sanadetsa zovala zawo; ndipo adzayenda ndi Ine m'zoyera; chifukwa ali woyera"*

Kumbukirani kuti awa ndi othawa. Iwo anathawa, koma iwo kwenekweni sanapite mu chimene Mulungu amafuna, chimene chimayenera kuyenda limodzi ndi kuwala kwa uthenga mu m'bado wina kapena kusuntha kwa Mulungu. Panali ena, kotero, amene anali oyenera kuyenda ndi Mulungu.

Mulungu anauza m'bado wa Sarde kuti uyende moyenera. Wina anati zilibe kanthu kaya tikhala moyo wabwino kapena ayi, ife tinadziwidwiratu. Ngati inu simukhala moyo wolondora zimenezo zikuwonetsera kuti inu simunadziwidwiretu. Baibulo likuti ife tinadziwidwiratu kuti tikhale mu chifanizo cha Mwana Wake. [Aroma 8:29] Ngati moyo wanu sunasandulike kukhala mu chifanizo cha Mwana wake, inu mungatsimikizire bwanji kudziwidwiratu kwanu? Pamene inu musandulika chifanizo cha Yesu Khristu, kenako inu mukhoza kunena kuti munadziwidwiratu.

Vesi 5: *"Iye amene alakika adzamveka motero zobvala zoyera, ndipo sindidzafafaniza ndithu dzina lache m'bukhu la moyo, ndipo ndidzavomereza dzina lache pamaso pa atate anga, ndi pamaso pa angelo ache."*

Panali ogonjetsa mu m'bado uli wonse .M'bado uwu unabwerera ku dziko monga m'bado uli wonse, koma mbewu imeneyo inapitirira, pamene nansongole anabwerera mu njira zake, chimene chinali kupanga chipembedzo.

Gawo lotsiriza la vesi 5 likuti: *"Ndipo sindidzafafanizani ndithu dzina lache mbukhu la moyo, ndipo ndidzabvomereza dzina lache pamaso pa Atate anga, ndi pamaso pa amngelo ache."* Ichi ndi chitonthozo ndi chitsimikizo chodala."

Panali ena amene amagonjetsa mu m'bado uliwonse ndipo iwo adzauka mu chiukitsiro choyamba, ndipo ife tidzakumana nawo ndiye tidzakhala pamodzi ndi kutengedwa mlengalenga kukakumana ndi Ambuye.

Ena anagonjetsa mu m'bado wa Sarde ndipo sanadziwe chilichonse koma *"Olungama adzakhala ndi moyo mwa chikhulupiriro.***" Iwo unali Mzimu Woyera mu m'bado umenewo.**

Vesi 6: *"Iye amene ali ndi khutu amve chimene Mzimu anena kwa mipingo."*

Mulungu sakunena za khutu la thupi. Iye akunena za iwo amene angamve vumbulutso ndikuzimvetsa. Njira yokhayo mungathe kuzimvetsa ndi pokhapo ngati zinaperekedwa kwa inu maziko a dziko la pansi asanakhale kuti muzimvetse.

M'bado wa Filadelfeya 1750-1906

Vesi 7: *"Ndipo kwa mngelo wa ku Filadelfeya lemba; Izi anena Iye amene ali woyera, Iye amene ali woona, Iye wakukhala nacho chifungulo cha Davide, Iye wotsegula, ndipo palibe wina atseka; Iye wotseka, ndipo palibe wina atsegula."*

M'bado uwu unali m'bado wa Filadelfeya. Unakhala kuchokera mu 1750 mpaka 1906. Yohane Wesile ndi amene anali wam'thenga wa m'bado uwu. "Filadelfeya" amatanthauza *"chikondi cha pa abale,"* choncho uwu unali m'bado wa chikondi cha pa abale. Uwu unali m'bado waukulu wa umishonare umene sitinawumvepo.

"Izi anena Iye amene ali woyera." Uwu ndi m'bado umene unabweretsa ungwiro ndi chiyero. Ngati inu muli mu chiyanjano ndi Mulungu, mukuyenera kukhala angwiro. Mukakhala moyo woyera, kukhulupirira Mau a Mulungu, ndiye inu mwayeretsedwa. Inu mumayeretsedwa pamene Iye amene ali woyera abwera mwa inu ndipo ntchito za thupi zimathawa. Tsopano chiyero chimenecho sichingakhale chilungamo chanu. Chikuyenera kukhala chilungamo cha Khristu, pamene Mzimu wake ubwera mwa inu. Lotsatira la vesi 7 likuti, *"Iye wakukhala nacho chifungulo cha Davide, Iye wotsegula, ndipo palibe wina atseka, Iye wotseka ndipo palibe wina atsegula."* Chimodzi mwa ntchito za Davide zinali kuti Iye anali wa nkhondo. Iye akapita ku nkhondo, amapambana. Tsopano, Mulungu wapereka chifungulo cha Davide ku mpingo. Pamene Iye akhala nayo ntchito kuti achite kapena nkhondo kuti agonjetse, Iye amangokupatsani inu chifungulo cha Davide.

Pamene inu mukhala mu nkhondo yovuta ndipo zikuoneka ngati simungapambane inu mungofikira ndi kutenga chifungulo cha Davide ndi kugwiritsa ntchito icho. Icho sichingalephere.

Ine ndikufuna ndikuonetseni khomo lotseguka limene vesi ili likukamba. **Mpingo wa Katolika unalamulira kumadzulo kwa Ulaya. Anali ndi khomo limenelo lotseka, palibe aliyense amene anayesera kuchitsegula, koma Yohane Wesile, kapena mngelo, anatenga chifungulo cha Davide ndi kutsegula chitseko chimenecho. Mpingo wa katolika wa Chiroma unagonjetsedwa ndipo papa anachotsedwa pa mpando mu 1798.** Iwo anatsala pang'ono kuchotsa upapa, koma anamulora wang'ono kukhala pa mpando. Zinapitirira mu maonekedwe ovulala, mpakana pamene zinayamba kuchira kumayambiriro kwa zaka za ma 1900, mpakana pamene zinayamba kuchira pamene atsogoleri a dziko lapansi anayamba kuzindikira papa wa ku Roma. Mu 1700 ndi 1800, mpingo wa chikatolika wa Chiroma

mwantheradi unalibe mphamvu pa anthu. Chifukwa? Mulungu anatenga chifungulo, kutsegula khomo, ndikuwauza anthu alalikire dziko lapansi. Iwo anachita zimenezo. Mulungu anatsegula chitseko cha uthenga. Uthenga unayenda kuzungulira dziko lapansi, ntchito yochuluka ya umishonare inachitika ndipo uthenga unasindikizidwa mochuluka mu m'bado uwu kusiyana ndi m'bado wina uliwonse.

Kotero, Mulungu anati tsiku lina chitseko chidzatsekedwa. Mulungu wapereka ulaliki mu m'bado ndipo Iye atseka chitseko ndipo sichitsegulidwanso pokhapokha kwa 144,000, monga zaonetseredwa mu chaputala 14 cha bukhu ili.

Chitseko chatsekedwa mu malo ambiri, pokhapokha Mulungu ali ndi china chake kwa mkwatibwi wake kuti alowe m'menemo ndi uthenga wa chivumbulutso chaputala, 10:8-11. Mpingo udakali ndi chifungulo ndipo ife tikhoza kutsegula chitseko, monga Mulungu akufunira izo, koma nthawi yolalikira yaikulu yatha. Mulungu akufikitsa Oyeramtima ku ungwiro. Iye anapereka fanizo mu chaputala 13 cha Mateyu pamene ukonde unayikidwa ndipo anakhala pansi, kuonetsa kutha kwa m'bado uno.

Vesi 8: *"Ndidziwa ntchito zako, taona, ndapatsa pamaso pako khomo lotseguka limene munthu sakhoza kutsekapo, kuti uli nayo mphamvu pang'ono, ndipo unasunga Mau anga, osakaniza dzina langa."*

Mulungu anayika kwa mbewu iliyonse yodziwidwiratu khomo lotseguka, ndipo khomo lotseguka limenelo ndi Mau a munthawi. Inu mukhoza kuyenda mu icho ndipo mdierekezi sangakuletseni.

Gawo lotsiriza la vesi ili likukamba za kukhala ndi mphamvu pang'ono ndi kusunga Mau. Ngati tili nayo mphamvu pang'ono, Mulungu adzatsegula khomo, ndipo palibe munthu angatseke icho. Baibulo likuti Mulungu anachita kwa munthu aliyense muyeso wa chikhulupiriro. Iye anatsegula khomo ndikukupatsani inu mphamvu pang'ono, ndipo Iye akufuna inu musunge Mau ake. Kusunga Mau a Mulungu ndi kofunika. **Inu mukasunga Mau, chitseko chidzakhala chotseguka kwa inu.**

Mpingo wa ku Filadelfeya ku Asia mu tsiku la Yohane unali ndi dzina la Ambuye, chifukwa akuti, *"sunakaniza dzina langa."* Mipingo isanu ndi iwiri ku Asia imabatiza mu dzina la Ambuye Yesu Khristu. Iwo amasunga Mau. Mpingo uwu ku Filadefiya unali ndi mavuto, koma Mulungu anali nawo ndipo anasiya khomo lotseguka kwa iwo. Mpingo uwu unasunga Mau, ndipo sunakaniza Dzina Lake, ndipo unapitirira.

Kotero mu m'bado kuchokera 1750 mpaka 1906, dzina la Ambuye silinali lowululika mochuluka mu mau. Mu m'bado wa kukonzanso, amabatizabe mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Zinali mwa patalipatali anthu kumabatizidwa mu dzina la Ambuye Yesu Khristu, koma pamene tikamba za mpingo uwu mu mzinda wa Filadelfeya, anali ndi dzina la Ambuye.

Komanso, zimene adanena ku mpingo uwu Iye akunena kwa onse. Iye akufuna onse abatizidwe mu dzina la Yesu Khristu.

Vesi 9: *"Taona, ndikupatsa ena otuluka m'sunagoge wa Satana akudzinenera okha ali Ayuda komatu anama, taona, ndidzawadzetsa alambire pa mapazi ako, nazindikire kuti Ine ndakukonda."*

Sunagoge ndi kachisi wa chiyuda. Pamene Yohane amalemba izi zimagwirana bwinobwino, chifukwa panali ma sunagoge ambiri mu Asia, chifukwa Ayuda anali atamwazikana mu Asia Minor; koma pamene tizibweretsa mu tsiku lathu, sunagoge wa satana ndi mpingo umene sulemekeza Mau a mu tsiku ili.

Mu mpingo woyamba, akhristu amayamikira Ayuda, chifukwa kupyolera mwa Ayuda munachokera Messia monga mwa thupi. Iye anali mbewu ya Davide. Ichi chafotokozedwa mu chaputala 12 cha bukhu ili.

Mu mzinda uwu wa Filadelfeya, panali ena amene amati ndi Ayuda amene sanali Ayuda, koma mu m'bado uno ndi iwo amene amati ndi akhristu ndipo sali akhristu.

Ine ndikukhulupirira kuti mpingo uwu usanachoke pa dziko, Mulungu adzawuonetsera iwo, kuti mkhristu aliyense woona akhoza kudziwa chimene Mulungu akuchita. Iye adzakhoza ngakhale kulora mpingo wabodza uwone ndi kudziwa kuti Mulungu amakonda mpingo woona. Chifukwa ichi chikuti, *"Ine ndidzawapanga iwo kubwera ndi kupembedza pa mapazi anga, ndikuti adziwe kuti Ine ndakukonda*

iwe." Mulungu adzalora mpingo wabodza kudziwa kuti Iye amakonda iwo amene ali Ake, makamaka mkwatibwi wa Amitundu amene watulutsidwa mu zipembedzo.

Vesi 10: *"Popeza anasunga mau a chipiriro changa, Inenso ndidzasunga kukulanditsa mu nthawi ya kuyesedwa, ikudza pa dziko lonse lapansi, kudzayesa iwo akukhala padziko."*

Mulungu akufuna anthu amene adzakhala opirira, kumukhulupirira Iye, kuyenda ndi Iye, ndi kutenga chimene Iye akunena ndi kukhala mwa chimenecho.

Pamene moto unayamba kuzima mu Pentekosite wamakono ndipo anabwerera ku dziko, zimaonetsa kuti iwo anangotengeka. Ngati inu muli ndi Mau, adzakugwirani inu kaya mukumva chinachake kapena ayi.

Pali vumbulutso loti mukhoza kulandira Mzimu Woyera mopanda kutengeka, mopanda kulankhula malilime, ndi zina zotero. **Mulungu akufuna inu mukhale opirira ndi kusunga Mau ake.**

Vesi ili likuti, *"Inenso ndidzakusunga kukulanditsa mu nthawi ya kuyesedwa, ikudza pa dziko lonse lapansi, kudzayesa iwo akukhala pa dziko."* Ulosi uwu ukufalikira mpaka mu nthawi ya chisautso. Mulungu akulankhula, osati kwa mpingo uwu wokha ku Asia, kapena kwa m'bado uwu wokha, koma akulankhula kwa mpingo wonse, chifukwa chisautso chikubwera kumapeto, Mkwatulo utapita.

Vesi 11: *"Taona ndidza msanga; gwira chimene uli nacho kuti wina angalande korona wako."*

Ife tikufuna tigwire malo amene Mulungu watipatsa ife. Kodi Mulungu wakupatsani inu malo mwa Iye? Kodi Iye wakupatsani inu mwinjiro? Kodi Iye wakupatsani inu malo mu thupi? Ndiye inu gwiritsitsani.

Vesi 12: *"Iye wakulakika ndidzamuyesa iye mzati wa kachisi wa Mulungu wanga, ndipo kutuluka sadzatulukamonso, ndipo ndidzalemba pa iye dzina la Mulungu wanga, ndi dzina la mzinda wa Mulungu wanga, amene ndi Yerusalemu watsopano, wotsika mwamba, kuchokera kwa Mulungu wanga, ndipo ndidzalemba pa iye dzina langa la tsopano."*

Pamene mukhala mkhristu mpakana pakuti Mulungu akhoza kuika udindo pa mapewa anu, ndiyeno inu simuli wotuluka ndi wolowa. Iye anati inu simudzatulukanso kunja. Kodi kachisi wa Mulungu ndi chiyani tsopano? Ndi mpingo Wake [kachisi wauzimu] ndipo ukutchulidwa apa. Mu chaputala 11 cha Chivumbulutso, kachisi amene adzamangidwanso ndi kachisi wa thupi wa Mulungu.

Masiku ano, timaona anthu kulowa ndi kutuluka mochuluka moti samadzakhala mzati. Iwo sangakhale kapena mwala mu kachisi ngati sangakhale mkati. Iye anakuikani inu mu kachisi ngati mwala wa moyo ndipo inu mukuyenera kukhala pamenepo. **Mulungu safuna iwo a mu kachisi Mwake amene ali wolowa ndi kutuluka, mwamba ndi m'musi. Mipingo ya zipembedzo imawafuna iwo m'matchalitchi awo, chifukwa zonse zimene akufuna ndi gulu basi.** Mulungu sakhudzidwa ndi kuchuluka. Iye anamudziwa aliyense amene adzakhale pamenepo maziko a dziko lapansi asanakhale.

Vesi 13: *"Iye wakukhala nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa mipingo."*

M'bado wa Laodikaya 1906-Mpakana?

Vesi 14: *"Ndipo kwa mngelo wa mpingo wa ku Laodikaya lemba; Izi anena Ameniyo, mboni yokhulupirika ndi yoona, woyamba wa chilengo cha Mulungu."*

Tsopano tikulowa mu m'bado wa Laodikaya. Ine sindikuuzani zambiri za m'bado uwu, chifukwa inu mukukhala mu iwo ndipo mukutha kuona zimene zikuchitika. M'bado uwu unayamba mu 1906. "Laodikaya" ali ndi tanthauzo loti *ufulu wa anthu*. Aliyense akufuna ufulu wake. Inu muli ndi Mau a Mulungu, amene ndi maufulu amene Mulungu amakupatsani inu, ndipo iwo ali apamwamba.

Paulo anati inu muli ndi ufulu, musachite nawo ufulu chothandizira thupi. [Agalatiya 5:13] Mau akuti inu simuli ainu eni, koma mwagulidwa ndi mtengo wake. [1 Akorinto 6:20] Inu simumakhala a inu nokha. Paulo anati ku Agalatiya 2:20- *"Ndinapachikidwa ndi Khristu; koma ndiri ndi moyo; wosatinso ine ayi; koma Khristu ali ndi moyo mwa ine."*

Tsopano, ma ufulu a anthu ali kuti? Iwo akuikidwa mu Mau a Mulungu. Mulungu anaika utumiki mu mpingo ndipo iwo umaphunzitsa mkwatibwi weniweni maufulu amene Mau a Mulungu amawapatsa iwo. Iye anati anapatsa ena atumwi, ena aneneri, ena alaliki, ndi ena abusa ndi ena aphunzitsi kufikitsa oyeramtima ku ungwiro ndi ku ntchito ya utumiki. [Aefeso 4:11-12] Ntchito ya utumiki ikutanthauza ma udindo onse asanu, osati umodzi. Mulungu ali ndi utumiki usanu umene udzatsogolera mkwatibwi ku ungwiro umene Mulungu analonjeza ndipo ukugwira ntchito pamodzi pa cholinga ichi.

Vesi 14: likuti *"Izi anena Ameniyo."* Izi zikuonetsera umulungu wa Khristu. Vesi ili likutanthawuza kuti vumbulutso lakuti Mulungu ndi ndani, mu tsiku lotsiriza ili lidzabweranso ku mpingo. Ife tidzadziwa kuti Yesu si munthu wachiwiri. Iye ndi munthu yekhayo mu umulungu. Iye ndi yekhayo. Ndicho chifukwa mu m'bado uwu, mngelo wauzimu [mngelo wa chisanu ndi chiwiri] anabwera ndikubweretsa vumbulutso ili. **Kotero, m'bale William Branham, wam'thenga wapansi wa m'bado uno, m'neneri wa Malaki 4, anabwera ndi kulalikira umulungu wa Yesu Khristu.** Iye anatenga chidziwitso chimenecho kuzungulira dziko lapansi kasanu ndi kawiri, ndi uthenga kuonetsera kuti Yesu ndi Amen Wankulu ndi Wokhulupirika ndi Mboni yoona yamu vesi 14.

Vesi 15: *"Ndidziwa ntchito zako, kuti suli wozizira kapena wotentha: bwenzi utakhala wozizira kapena wotentha."*

Ili ndi limodzi la machimo a m'bado uwu; iwo uli wozizira kapena wotentha. Mwa kulankhula kwina, ngati inu mutangopembedza Mulungu mwa theka, theka mkati ndi theka kunja, ndiye Yesu akufuna inu mukhale mkati kapena kunja ndipo wosangokhala chophunthwitsa. Ngati inu mutangomuona winawake akuyamika Mulungu, akupfuula chigonjetso, ndikumalankhula malilime lero, ndipo mawa ali kunja ku malo omwera mowa, iwo ali chophunthwitsa ku cholinga cha Mulungu.

Vesi 16: *"Kotero, popeza uli wofunda, wosati wotentha kapena wozizira, ndidzakulavula m'kamwa mwanga."*

M'bado uwu ukulavulidwa mkamwa mwa Mulungu chifukwa iwo suli wozizira kapena wotentha. Mulungu akuti zimampanga Iye kudwala m'mimba mwake. Mulungu wadwala nawo m'bado wa mpingo uwu. **Iye adzausanza ndi kubwerera ku Israeli.** Ine sindikukamba za mkwatibwi. Mu m'bado uliwonse pali mpesa weniweni ndi mpesa wa bodza. Mpesa wabodza umalavulidwa mkamwa mwake, pamene mpesa woona umafika ku chidzalo cha Khristu ku m'bado.

Vesi 17: *"Chifukwa unena kuti ine ndine wolemera, ndipo chuma ndiri nacho, osasowa kanthu; ndipo sudziwa ndiwe watsoka, ndi wochititsa chifundo, ndi wosauka, ndi wakhungu, ndi wausiwa."*

Amenewo ndi maonekedwe a mpingo mwauzimu. Ine sindikukamba za mkwatibwi amene ali ndi vumbulutso. Ine ndikukamba za m'bado wa Laodikaya. Chimene chinayamba ndi Lutera, Wesile, ndipo ngakhale m'bado uno chili pompano ndipo changofika pofunda kuti chilavulidwe mkamwa mwa Mulungu. Iwo amati ndi achuma ndipo sasowa kanthu, koma pa maso pa Mulungu iwo ndi osauka, akhungu, ndi amaliseche ndipo sadziwa izo. Inde m'bado uwu ndi wa chuma ku zinthu za thupi, ndi matchalitchi awo akuluakulu kapena mau abwino apa ndi akuti, **"zimanyumba zazipembedzo." Ndi Edeni wa satana.** Mulungu akukana chivundi chonsechi cha zipembedzo, izo zilibe ntchito, koma kuti zidzaotchedwe mu chisautso.

Vesi 18: *"Ndikulangiza Ine ugule golide woyengeka m'moto, kuti ukhale wa chuma, ndi zovala zoyera kuti ukadziveke, ndi kuti manyazi a usiwa wako asaoneke; ndi mankhwala opaka m'maso mwako, kuti ukaone."*

Petro anati kuyesedwa kwa chikhulupiriro chanu ndi kwapamwamba kuposa golide woyesedwa ndi moto. [1Petro 1:7] Ichi ndi chikhulupiriro chimene chabwera kudutsa mu mibado iyi yonse. Ngakhale mu mayesero woopsya chikhulupiriro ku Mau a Mulungu chakhala chikuima. Mulungu adzakupatsani inu chikhulupiriro chenicheni mu Mau a Mulungu, chikhulupiriro mwa Yesu Khristu, chikhulupiriro mu mphamvu ya Mulungu, ndi chikhulupiriro mu utumuki ngati mungaulandire. Iye adzakupatsani inu golide amene wayesedwa mu moto.

Mulungu akulankhula mu vesi ili kuti Iye amakulangizani inu mutenge chinachake kwa Iye chimene ndi chenicheni. **Pali ubatizo weniweni wa Mzimu woyera. Sikwenikweni kungolankhula malilime, koma kukhulupirira kuti Ambuye Yesu Khristu ali mwa inu, kuulura Mau a Mulungu kwa inu. Ndi chimene Yesu akufuna akupatseni inu. Anthu sakufuna zimenezo; iwo akufuna chinachake chokhala ngati zotengeka.**

Mulungu akuuza m'bado uno kuti Iye ali nacho chenicheni ndipo iwo sakuyenera kukhala ndi chongoyerekezera kapena chongovala. Iye ali ndi china chake chenicheni ku mpingo. Chifukwa chiyani winawake akufuna chimene sichili chenicheni pamene mlengalenga mwadzaza ndi chenicheni? Ichi ndi chimene Mulungu akuuza mpingo.

Kodi Iye anatumizira ndani golide wa pa vesi 18 mu m'bado uwu wa Laodikaya? Palibenso wina koma wam'thenga wa m'bado uno, William Branham. Iye anabwera ndi Uthenga weniweni wa Mzimu Woyera. Iye analalikira Mau a Mulungu, ndipo Mulungu analemekeza izo kuzungulira dziko lonse. Munthu uyu anabweretsa vumbulutso loona ku mpingo. Iye anabweretsa Mau amene ayesedwa kudutsa mu mibado. Anthu azikana ndi kuzinyoza, koma Mulungu wazilemekeza izo.

Vesi 19: *"Onse amene ndiwakonda ndiwadzudzula ndi kuwalanga, potero chita changu nutembenuke mtima."*

Ichi ndi chimene Mulungu adzachita kwa inu ngati muli mwana wa Mulungu ndipo mukuyenda kunja kwa mzere. Ngati Mulungu angakudzudzuleni ndi kukulangani inu, inu musamubwezere Mulungu. Ndi chikondi chimene chimamupanga Iye kukukonzani inu, kotero mu zinthu zonse, mumuyamike Iye. Vesi 20: *"Taona ndaima pakhomo, ndigogoda; wina akamva Mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwa iye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi Ine."*

Tsopano chimene ndikufuna kuti muone apa, ndi chakuti pakubwera nthawi kumapeto a mibado pamene Khristu salinso mu mibado ya mpingo. Iyi ndi nthawi yaing'ono imene Iye akuchita kopambana ndi mkwatibwi. Iye akuima kunja kwa mabungwe ndipo Iye akugogoda m'mitima ya anthu kupempha kuti alowe miyoyo yawo kuti Iye akhale m'modzi ndi iwo.

Mu chaputala choyamba cha Chivumbulutso, Iye akuzindikirika ngati Wansembe Wankulu akuyenda pakati pa zoikaponyali. [Chivumbulutso 1:13] Kupatula zimene zinachitika mu mibado imeneyo, Iye nthawi zonse amayenda pakati pa zoikaponyali. Iye amakhala mu mpingo mu kagawo ka Mzimu Wake.

Tsopano ku mapeto kwa m'bado Mngelo Wankulu wa Chivumbulutso 10:6 anakweza dzanja lake kumwamba ndi kulumbira kuti sipadzakhalanso nthawi. Izi zikutanthauza kuti kulibenso nthawi kwa ana a hule akazi, palibenso nthawi kwa mibado ya mipingo, ndipo palibenso nthawi kwa hule mayi wachikulireyu. Tsopano, Yesu amadzipanga yekha weniweni kwa gulu lapadera la anthu, ndipo iwo ndi Mkwatibwi Wake, iwo amene ndi woona ku Mau.

Vesi 21: *"Iye wakulakika, ndidzapatsa akhale pansi ndi Ine pa mpando wa chifumu wanga, monga Inenso ndinalakika, ndipo ndinakhala pansi ndi Atate wanga pa mpando wa chifumu wache."*

Taonani, Chivumbulutso 3:21, chikuti *"Kwa iye amene alakika."* kulakika chiyani? Chimodzi cha zochitika za mu m'bado uno ndi kufunda, ndipo Iye anati, *"chifukwa chakuti uli wofunda Ine ndidzakulavula mkamwa mwanga."* [Chivumbulutso 3:16] Iye akufuna ife tikhale wotentha kapena wozizira. Apa akuti, *"Kwa iye amene alakika ndidzampatsa akhale pansi ndi Ine pa mpando wa chifumu wanga."* Gwiritsitsani ku chimenecho chifukwa tizipeza zimenezo mu chaputala 4, pamene zikuonetsera kwenikweni Yesu akukhala pa malo a Atate kapena pa mpando wa chifumu wa Mulungu.

Izi sizikutanthauza kuti wolakika adzapita kwa Yesu ndikumuuza Iye kuti achoke kuti iwo akhale ndi Iye. Zikutanthauza kuti wolakika adzagawana mu ulamuliro wa Yesu Khristu. Lotsatira la vesi 21 likuti, *"monga inenso ndinalakika ndipo ndinakhala pansi ndi Atate wanga pa mpando wa chifumu wache."* Yesu Khristu mwiniyekha amayenera kukhala wolakika. Yesu analakika motani? Inu mutati muphunzire moyo wa Yesu, inu mudzapeza kuti Iye amayenera kulakika mu zinthu zambiri. Ku Ahebri 4:15 akuti Iye *"wayesedwa mu zonse monga momwe ife."* Komanso, Ahebri 2:14 akuti *"Popeza tsono ana ndiwo a mwazi ndi nyama, Iyenso momwemo adalawa nao makhalidwe amwewonso kuti mwa imfa akamuononge*

iye amene anali nayo mphamvu ya imfa, ndiye mdierekezi." Iye anakhala munthu ndi kusiya pambali umulungu [Afilipo 2:7-8] nakhala kapolo, munthu, ndipo anakhala moyo zaka makumi atatu mphambu zitatu [33] ndipo amayenera kulakika. Kotero, ife tikuyenera kukhala wolakika mu nthawi iyi.

Mu chaputala cha 4 inu mudzamuona Iye ngati wolakika ndi Iye akukhala pa mpando wa chifumu ndi Atate wake, ndipo inu mudzaona lonjezano la kwa wolakika.

Vesi 22: *"Iye wakukhala nalo khutu amve chimene Mzimu anena kwa Mipingo."*

Mu m'bado wa mpingo uwu wotsiriza, monga mibado ina yonse, zimatengera vumbulutso la uzimu kuti mumve chimene Khristu akunena ku Mpingo Wake.

Mochuluka ndi mochuluka zimatengera vumbulutso kuona Mau a Mulungu, monga mudzaona mumachaputala ena a bukhu ili la Chivumbulutso. Koma, *"Iye amene ali ndi khutu"* adzamvetsa bukhu ili pamene likufutukuka pamaso anu odabwitsa. Amen.